


# BUKHU LA MOYO

## WA MWANAWANKHOSA

 Mmawa wabwino, abwenzi. Zinali ngati zodabwitsa kwa ine kukhala pano lero. Ine sindimayembekeza kuti ndidzakhala kuno. Ine ndimayenera kuti ndikakhale ku Kentucky. Ndipo mzanga wokonedwa kwambiri anadwala mowopsya, M'bale wathu Lyle McSpaddin. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . chikhaliidwe chakuti akufa mchipatala. Akazi a Fergerson amene anakonda kubwera kuno, mwana wawo wamwamuna akufa, nayenso, mchipatala. Ndipo chotero ine sindinapite, ndipo ndinangokhala chifukwa cha iwo.

<sup>2</sup> Ndipo kenako Bambo Matheny a mpingo wa Pentekoste mu New Albany, pa Silver Street, kungodutsa a . . . Ndi pakati . . . Ndi pa Oak and Silver, ine ndikuganiza. Ndipo iye . . . Ine ndimayenera kuti ndimuyankhulire usikuuno, ndipo ine ndinamuza iye . . . Ndinazisintha izo, Lachitatu lapitali, ndipo ndinamuza iye kuti ine ndidikirira mpaka ine ndidzabwerere kuchokera ku Indianapolis. Ndipo kenako basi pamene ine ndimathamangira ku chipatala dzulo, kuti ndikamuwone M'bale Lyle, bwanji, ine ndinakumana naye iye. Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndaona kuti inu simunapite.”

Ndipo ine ndinati, “Ayi.”

Iye anati, “Chabwino, bwerani, mudzayankhule, mulimonse.”

<sup>3</sup> Chotero, ine ndikuganiza, Ambuye akalola, ine ndikakhala kumusi kumeneko usikuuno, kuti ndikamuyankhulire M'bale Matheny. Ndipo, eya, ine ndinamuza iye, kuti pamene ife tikadzapita kumeneko, ine ndikanati ndidzakhale ndi msonkhano wa machiritso kwa iye. Ndipo ine kawirikawiri ndimakonda kusala pafupifupi masiku atatu msonkhano wa machiritso usanachitike. Chotero ine ndinamuza iye kuti ndikayankhula, ndipo ngati aliyense kumeneko, ife tikawapempherera iwo, mulimonse, basi a—mzere wapemphero wanthawizonse.

<sup>4</sup> Tsopano, ife tiri ndi sabata limodzi lina, sabata kuchokera Lolemba likubwerali, tsopano kuti misonkhano iyambike ku Cadle Tabernacle mu Indianapolis. Ndipo ife tikudalira kuti Ambuye akatidalitsa ife kumeneko, mu msonkhano wopambana waukulu. Monga mwana, akuyembekezera Khrisimasi, ine ndikuyembekezera msonkhano umenewo. Ine . . .

<sup>5</sup> Inu, basi chinachake chokhudza kutumikira Ambuye, ife timatopa kwambiri nthawi zina, mpaka izo zimawoneka ngati ife sitingapite patsogolo paliponse. Ndiyeno pamene iwe upuma, tsiku limodzi kapena awiri okha, pamakhala chinachake chimakukhudza iwe ndipo—ndipo umangoyenera kuti upitenso kachiwiri. Chotero, lero, ife tiri pano ndi cholinga chimodzi, ndicho, kutumikira Ambuye.

<sup>6</sup> Ndipo basi ife tisanakhale ndi pemphero ndi kuwerenga kwa Mawu, ine ndikufuna kuti ndipepese poyera kwa M'bale Neville. Ine...Dzulo, ine ndinakhala kunyumba kuchokera ku Kentucky, dzulo, ndicholinga, chakuti ndidzalalikire mmalo mwa iye pa wailesi. Loweruka likubwerali, ndipo Mulungu akalola, ndipo M'bale Neville akalola, Ine ndikufuna kuti ndidzayankhule pa kuwulutsa kwa mmawa Loweruka likubwerali, mmalo mwa M'bale Neville.

<sup>7</sup> Ndipo chotero, iye anali wachisomo kwambiri kuti andikhululukire ine, mophweka. Iye anati...Ndikuganiza kuti ndinapezerapo mwayi pa iye, ndipo iye ndi mmodzi wa anthu amene ndingati...Ine ndikhoza kumubwezera zoyamikira, ndipo, "Kuyembekezera winawake." Ndipo chimene chinandisokoneza ine chinali molawirira mmawa umenewo pamene iwo anandiyitanira ine kwa M'bale Lyle ndi iwo, mu New Albany. Ndipo ine...Iwo anali pafupifupi maminiti teni kuti ikwane naini koloko, ndipo ine ndinati, "Oh, ine ndimayenera kukhala pa kuwulutsa uko mu maminiti teni." Ndipo kuno, ine mu Jeffersonville, iye kumusi uko akundiyeembekezera ine. Chotero ine...

<sup>8</sup> M'bale Wood anamuyimbira iye dzulo, ndipo ine ndinaganiza ndimulola M'bale Wood andipepesere ine, poyamba, inu mukudziwa. Chotero iye anangondipatsa chilango kundipangitsa ine kuti ndidzayankhule mmawa uno, kuti ndibwere kuno. Chotero apa ife tinali. Ndipo chotero iye... ndife...

<sup>9</sup> Ife tikudalira kuti—kuti Mulungu adza—akhala mmisonkhano yathuyi. Ine ndiribe chimene ndakonzeratu; sindikudziwa nkomwe poyambira mu Lemba; ndinangotola Baibulo langa mphindi zingapo zapitazo, ndi kumathamangira kuno. Ine ndinachita kutenga Baibulo langa la Collins, chifukwa ilo liri ndi zilembo zokulirapo.

<sup>10</sup> Mai! Ine ndadutsa forte, inu mukudziwa. Chotero, pamene iwe ufika usinkhu wa zaka forte, chirichonse chokuyandikira iwe, iwe sumachiwona icho monga iwe unkachitira, inu mukudziwa. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi zoonza? Eya. Inde, bwana.

<sup>11</sup> Kuno osati kale kwambiri, ine ndinaganiza, "Kumati, pali chinachake cholakwika ndi ine, Ine sindingavale magalasi obiriwira kapena magalasi ofiirira." Ine sindimatha;

zimandidwalitsa mmimba mwanga. Chotero ine ndinati, “Pali chinachake cholakwika.” Ine ndinamuyimbira Dr. Adair, ndipo ine ndinati, “Doc, ndi a mtundu wanji. . .Kodi mungandiyenze maso anga, ndiuzeni ine mtundu wa magalasi amene ndikuyenera kukhala nawo?”

<sup>12</sup> Iye anati, “Ine, ndikhoza kukuuzani inu chiyani.” Anati, “Ine ndikuuzani inu. Ine ndingokutumizani inu ku Louisville, kwa katswiri wina kumeneko, wa zimenezo.”

<sup>13</sup> “Chabwino,” ine ndinati, “Ine sindikufuna kuyeza maso.” Ine ndinati, “Ine ndiri ndi maso abwino. Ndikhoza kuyima ndi kuliwona tsitsi liri pansu.”

<sup>14</sup> Iye anati, “Koma, kulibwino akakuyezeni inu, mulimonse, ndipo iye akakuuzani mtundu umene inu mukuyenera kukhala nawo.”

<sup>15</sup> Chotero, ine ndinapita kumeneko. Ndipo, ndinadzapeza kuti, iye anali m’bale Wachikhristu, ankafuna kuti abwerere ku Africa ndi ine ndi kumakachita maoparesoni ena. Anati, “Tsopano, mbadwa zimenezo ndi zosamvetseka kwambiri, mwaona.” Anati, “Iwo sangalole kuti mpeni uwadule iwo.” Koma iwo amakukondani inu. “Ndipo ine ndikufuna kupereka miyezi sikisi ya utumiki waulere, wochotsa ng’ala ndi zinthu monga choncho, kwa mbadwazo.” Ndipo iye anati, “Inu mukadzapita kumeneko,” anati, “Ndikufuna ndidzapereke miyezi sikisi ya moyo wanga ku utumiki wa Ambuye.”

Ine ndinati, “Doc, kodi inu mumakhulupirira mu machiritso Auzimu?” Iye anati, “Mawu aliwonse a izo.”

<sup>16</sup> Ndipo iye anandipatsa ine umboni, wa nthawi ina pamene. . .Iye anali katswiri wa pammero ndi maso. Iye anati iwo anamuimbira iye. Mwana wamng’ono anali atameza imodzi ya kherere zimenezo, ndipo iyo inadzakodwa pakhosi pake. Anati, “Ndinapita kumeneko, ndipo mwanayo anali akungopita. Iwo anathamangira naye ku chipatala. Panalibe chirichonse chimene mukanachita.” Anati, “Ine sindinadziwe choti ndichite. Chotero,” anati, “Ine basi, ngati, ndinatuluka mchipinda, ndipo ndinati, ‘Wokonedwa Atate Akumwamba, ndithandizeni kuti ndidziwe mwanjira ina choti ndichite kwa mwana wosaukayo. Iye akufa. Ndipo sindingathe kupeza chirichonse pomuzungulira iye, kumugwedeza iye, ndipo sindikudziwa choti ndichite.’” Ndipo anati, “Mwanayo anapita, ‘Uh!’ Ndipo kherereyo linawulukira pansu. Chotero,” iye anati, “ine ndingalephere bwanji kukhulupirira?” Pemphero limasintha zinthu. Uko nkulondola. Chotero, iye anandiiza ine. Iye tinakhala pamenepo ndi kuyankhulana kanthawi pang’ono.

<sup>17</sup> Ndipo iye anali ndi chipinda chaching’ono, chamdima, iye anali ndi chinthu chaching’ono chimene chinabwera pamenepo, ndipo ine ndinawona kuwala kwakung’ono kofiira. Iye anati, “Kodi mungawerenge zimenezo?”

<sup>18</sup> Ine ndikuchiwona icho chikuti twente-twente. Ine ndinati, “Inde, bwana.” Ine ndimatha kuwerenga icho, mulimonse, twente-twente. Kenako iye anayika fifitini-fifitini, ine ndimatha kuwerenga icho. Ndipo teni-teni, ine ndimatha kuwerenga icho.

<sup>19</sup> Anati, “Chabwino, mulibemo vuto lochuluka ndi maso anu.” Kenako iye anayika telesikopu yaing’ono kunja apa, ndi...Anati, “Ndiwerengereni ine chimenecho.” Ndipo ine ndinazindikira icho, ine ndimakhoza kuwerenga izo bwino bwino. Iye amapitirira kumayandikira, yandikira. Ine ndinayamba kuchepetsa liwiro la mawerengedwe anga. Pamene iye anadzafika pafupifupi monga *chonchi*, ine ndinasiya. Iye anati, “Ine ndikuuzani inu, ndisanakufunsemi inu. Inu munadutsa forte.”

Ine ndinati, “Inde. Izo nzoona.” Ine ndinati, “Ndiri ndi forte-faivi.”

<sup>20</sup> Ndipo iye anati—iye anati, “Chabwino, pamene munthu wadutsa forte...” Anati, “Ine sindikuwona momwe inu mwapiririra nazo nthawi yayitali *chonchi*.” Anati, “Monga momwe tsitsi lanu limachitira invi, khungu lanu limachita makwinya, tsitsi limabwera mmakutu mwanu, ndi zina zotero.” Bambo Egan akhoza kukuuzani inu zimenezo, monga wometa. “Ndipo pamene iwe udutsa usinkhu wa zaka forte,” anati, “maso anu amaphwa ndipo samatha madzi.” Anati, “Tsopano ndikuuzani momwe mungachitire izo. Chabwino, tsopano, inu muzifinya maso anu moyandikana pamodzi, ndi kumawerenga izo.”

<sup>21</sup> Chabwino, m’bale, ine ndimakhoza kuwerenga izo, ngati izo zikanakhala pafupi *chotero* kwa ine, kufinya maso anga. Kuyika manja anga monga *choncho*, ndi kupanga telesikopu yaying’ono, monga, inu mukukhoza kuwerenga izo. Palibe cholakwika chirichonse ndi maso anu. Ndi chirengedwe basi, usinkhu wa zaka forte zakubadwa, anthu amayenera kuti azivala magalasi owerengera.

<sup>22</sup> Ndipo *chotero* iye ankafuna kundipangira ine ena. Ndipo, chabwino, iye anatero. Koma ine—ine sindinazikonde konse zinthuzo, inu mwaona. Ndipo ine—ine nthawizonse sindimalingalira za iwo, ndipo ndimawerenga nthawizina. Ndipo, koma, ine ndangodzipezera Baibulo la Collins, limene liri a—ndi zilembo zazikulu pang’ono. Ndipo ndinaganiza, “Chabwino, ine sindingazolowere kuwavala iwo, inu mwaona.” Ndipo iwe si—iwe sumayang’ana...Ngati ine ndingayang’ane kumbali, monga *choncho*, iwe sungawone kalikonse. Koma iwe umayang’ana pansu pafupi, ndiye izo zimabweretsa izo kwa iwe.

<sup>23</sup> Anati, “Tsopano, ukayamba kuwerenga monga *chonchi*,” anati, “chinthu choyamba inu mukudziwa, iwe umakhala ukupitirira kumakankhira dzanja lako mmbuyo. Kutali

*choncho*, nkono wako siwautali mokwanira, kuti ungafikire kwa izo.” Chotero, umo—umo ndi momwe izo zimakhallira.

Ndipo chotero, tsopano, a—Ambuye adalitse.

<sup>24</sup> Tsopano ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake, mmawa uno, ife tisanayambe phunziro la Sande sukulu. Chiyani—kodi mtengo ndi chiyani? Ndakhala ndikulingalira pa izo. Ngati ine ndikanakhala ndi mmero wokwanira mmawa uno, ine ndikanalalikira pa phunziro limenero. Koma, mmero wanga, ndiwoyipa, ndipo ine ndiri ndi msonkhano uwu umene ukubwera kuno, New Albany, usikuuno. Ndiyeno, inenso, ine ndiri. . . Misonkhano ikuyambika. Ine ndikungofuna kuti ndiphunzitse kwa kanthawi, mmawa uno, kuchokera mu Lemba lina. Koma, kodi mtengo ndi chiyani?

<sup>25</sup> Amayi anga, sindikuganiza kuti iwo ali pano. Sindikuwawona paliponse. Iwo alipo? Inde, amayi, inu mukuchepa. Chotero, ine ndinawafunsa iwo dzulo. Ine ndinawafunsa iwo phunzirolo, chifukwa ine ndakhala ndikuliwerenga ilo. Kodi munakhalapo ndi chinthu mmaganizo mwanu, ndikuyamba kuwerenga? M’bale Weber, inu munachitapo izo nthawi zambiri, ndi kungoyamba kuwerenga.

<sup>26</sup> Kodi mtengo ndi chiyani? Ndipo ine ndinayamba kulingalira. Ine ndinati, “Inu mukudziwa, ngati ine nditakhala ndi madola handirede milioni atakhala apa pa mulu, ndipo nkukhala ndi batani laling’ono apa. Ngati nditakanikiza batani ili, ndingataye madola handirede milioni anga, koma ndingayambe kuyankhulana ndi abambo anga okalamba amene anapita, monga ora limodzi, munthu wachivundi kachiwiri. Ine ndingachite chiyani?” Osakayikira, ine ndingakanikize batanilo. Ine ndingapereke madola handirede milioni, mmawa uno, kuti ndiwakhazike abambo anga pansu pa mpando uwu, pamene ine ndikuphunzitsa phunziro ili. Chotero mtengo wa ndalama ndi chiyani? Kodi moyo ndi wochuluka bwanji kuposa ndalama? Mukuona?

<sup>27</sup> Tsopano, amayi, inu mukukumbukira pamene ine ndinali ndi Ford yaing’ono yakale ya T-model, yaing’ono yakale ’26 model? Momwe ndinkachipukutira chinthu chimenecho! Ine ndinali mwana chabe, pafupifupi usinkhu wa zaka sikisitini, seventini zakubadwa. Ndinali wochimwa nthawi imeneyo. Ndipo nthawizina. . . Ine ndinkagwira ntchito ndi Bambo Genter kumbuyo uko. Ndipo ndinka. . . Pambuyo pa Lamlungu masana. . . Lamlungu mmawa, ndinkapita kumusi ndi kukanola mano onse ndi zinthu, a kompresa ya mpweya, ndi kuyitsuka iyo. Lamlungu masana, ine ndinkapukuta Ford yaing’ono yakale ija, mpaka inkawoneka ngati penti ikanganukapo pa iyo. Bwanji ngati ine ndikanayesera, mmawa uno, kuti ndipeze chidutsa chimodzi cha Ford imeneyo? Bwanji ngati ndikanayesera kupeza chimodzi cha zidutsa zazing’ono, kuchokera pa kompresa

ya mpweya ija? Nthawi yomweyo ndikanakhala ndikupindula miyoyo, ndinkapukuta Ford yanga. Ndikudabwa komwe mtengo uli.

<sup>28</sup> Ndinkagwira ntchito Lamlungu mmawa kumtunda uko, monga momwe iwo ankandilolera ine. Ine ndinkayamikira zimenezo, chifukwa ndinali mu ngongole. Ndipo ine. . . Koma kuti—izo zinanditengera ine kuti? Kodi zinapindula chiyani?

<sup>29</sup> M'bale Ledford, bwanji ngati winawake atabwera kwa inu ndi ine, ndi M'bale Neville, mmawa uno, tonsefe pano, atatu a ife, kani, ndi kuti, “Atumiki, ndimupatsa aliyense wa inu madola millioni.” Winawake anali wachuma. . . akhoza kuchita izo.

<sup>30</sup> Ndipo ine nkuti, “Tsopano, M'bale Ledford, M'bale Neville, ine ndikukuuzani inu zomwe ife tichite. Tiyeni tipite tikawapeze anthu osauka onse omwe tingawapeze. Tiyeni tikapangitse nyumba yaing'ono iliyonse kusangalala, powagulira ana zovala, ndi kulipira ngongole ya nyumba, kapena kugula malo aang'ono awa. Sitidzaphonya konse izo. Madola millioni aliyense, bwanji, chiwongola dzanja pa izo, kusamalira ochuluka omwe ife tingakwanitse ndi zimenezo; kuyikamo chuma china chabwino kapena chinachake. Ndiyeno ife tingachite chiyani? Zimenezo zikhoza kukhala zabwino, kuti, osalola kuti aliyense adziwe kanthu za zimenezo. Mitima yathu ingakhutire.

<sup>31</sup> Koma, tsopano, mu zaka handirede kuchokera lero, abale, izo zingatengere chozizwitsa cha Mulungu, ngati ife tingakhalebe moyo zaka handirede kuchokera lero, inu mukudziwa zimenezo. Tsopano, ife tingakhale tiri ku Muyaya. Kodi madola millioni angachite chabwino chanji, kapena kudiyetsa osauka konseko, ndi zinthu zimene ife tazichita? Mukuona? Mtengo wake sungakhale wochuluka chomwecho. Ngati nditakhala ndi billioni, mmawa uno, izo zingatichitire ife ubwino wanji ife titapita?

<sup>32</sup> Koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Ife tiribe ndalama zimenezo. Ndinu munthu wosauka; tonsefe tiri. Uko nkulondola. Ife timakhala moyo ndi zithandizo za anthu, pokhala atumiki. Koma m'bale, mu Afrika, mnyamata mmodzi wamng'ono wakuda wausinkhu pafupifupi *chonchi*, kapena hule wa mu msewu uko mu Louisville, moyo umodzi utapulumutsidwa; mu Muyaya, pamene nyenyezi imeneyo izikawala kutsidyako, dzina lathu lidzakulungidwa mmenemo. Mtengo wanu ndi umenewo. Si zochuluka bwanji zimene muli nazo, zochuluka bwanji zimene mukuzikhumba. Ndi zochuluka bwanji zimene mungachite kuti mupulumutsire miyoyo kwa Yesu Khristu. Ndalama zathu zidzatha.

<sup>33</sup> Ine ndinkapukuta Ford yaing'ono yakale ija. Ndipo mmawa uno, yakhala uko mu garaja ndi Cadillac yomwe iwo anandipatsa ine. Koma limodzi la masiku awa, Cadillac imeneyo idzakhala momwe Ford iliri, iyo siidzakhaponso. Koma Mulungu

adzakhalabe yemweyo. Koma, ngati ine ndingapulumsire moyo kwa Khristu, m'bale, bola ngati kuli Muyaya, ulemelero wa Mulungu udzakhazikika pa moyo umenewo.

<sup>34</sup> Chotero, mtengo ndi chiyani, mulimonse? Iwo umachita ubwino wanji, pamene kulimbana kuli pakhosi panu, ndipo dokotala awona kugunda kukubwera pa dzanja panu? Kodi ndalama zonse ndi kutchuka ndi za ubwino wanji? Anthu oti azikusisitani pa nsana, kapena nkudzakhala munthu wamkulu, izo zimakuchitirani ubwino wanji? Osati mpang'ono pomwe. Izo zimatha, ndipo zimatsala pano pa dziko lapansi.

<sup>35</sup> Koma, moyo umodzi utapulumsidwa, inu mudzawona dzina lanu litakutidwa mmenemo, bola ngati nyenyezi ya mmawa idzakhala ikunyezimira mu mlengalenga. Chotero, tiyeni tipulumutse miyoyo, abale. Mmodzi aliyense, akazi apakhomo inu, inu simukusowa kuti mukhale mlaliki; inu muchite chinachake kwa ulemelero wa Mulungu. Kumbukirani, zinthu Zamuyaya ndi zomwe zimakhala kwanthawizonse, ndipo, ndiko, kupulumutsa miyoyo. Mulole icho chidzikhala chinthu choyambirira, cha ntchito zanu zonse ndi malingaliro anu onse ndi zolinga zanu zonse.

<sup>36</sup> Dzulo, nditayima chapafupi, nditagwira dzanja la amayi, nkono wanga mowakumbatira iwo, ndipo chibwano chawo chikunjenjemera.

<sup>37</sup> Ndipo mnyamata wake atagona pamenepo, akufa, iye anati, "Billy, ine—ine ndakhala ndikufuna ndi kufuna kuti inu mubwerere ku kachisi."

<sup>38</sup> Ine ndinati, "Mlongo Ferguson, ine—ine ndingakonde nditachita zimenezo." Iye anatero. . . Ine ndinati, "Chabwino, penyani, mlongo. Kumene ndingakhoze kupeza mwinamwake miyoyo fifite yopulumutsidwa, pa chaka, mu kachisi, izo zingakhale zokolola zabwino pa chaka. Ine ndikhoza kupulumutsa handirede sauzande a iwo mdziko lina. Mukuona?"

<sup>39</sup> Pamene ndizidzalowa mu Ulemelero, sindikufuna kudza. . . Mulungu adzandipulumutsa ine. Iye anandipulumutsa kale. Izo zakhazikika. Koma chinthu chake ndi chakuti, pamene ine ndidzafike kumeneko, ine ndikufuna kuti ndidzayang'ane pozungulira ndi kudzawona nyenyezi zikuwala. Amen. Ine—ine ndikufuna ndidzawone chinachake chimene chimapanga chinachake.

<sup>40</sup> Ngati ine—ngati ine ndikanafa, ndipo ine ndinali munthu wamkulu, purezidenti monga Lincoln, kapena chinachake chonga icho, iwo angadzamange, chikumbutso, chachikulu; koma tsiku lina icho sichidzakhhalapo. Koma moyo umodzi utapulumsidwa, mu Ulemelero, dzina lanu lidzakutidwa mmenemo, bola ngati kuli Muyaya ukuzungulira.

Chabwino, tiyeni tipemphere tsopano.

41 Atate athu Akumwamba, ife modzichepetsa tikubwera kwa Inu, mmawa uno. Mulungu, ndine wokondwa kuti ndinadzuka, pafupifupi zaka twente-faivi zapitazo, ku choona chakuti—chakuti chimwemwe sichipezeka ndi zinthu za dziko lino. Icho chimapangidwa ndi zinthu Zamuyaya, zomwe zimatipangitsa ife kukhala osangalala mmoyo wathu.

42 Ndipo ndine wothokoza bwanji, mmawa uno, ndi woyamikira kwa Inu, chifukwa cha chipulumutso Chanu ndi chisomo Chanu, chimene chandilola ine, Ambuye, kuti ndiwone pafupifupi miyoyo millionsi ikugwada pa guwa. O Mulungu, tsiku lina laulemelo, pamene ine ndidzawoloka, ine ndikuyembekeza kudzawawona iwo onse akuwala kumeneko, ngati nyenyezi. Abale anga apa, alongo anga, mmawa uno, mmodzi aliyense akumverera mwanjira yomweyo. Iwo anali gawo mu izo, Ambuye, kudzera mmapemphero awo ndi mapembedzero, ndi kugwiritsitsa kwa Mulungu; akupemphera, kuyankhula ndi ena, ndi kuyankhula mokweza za zinthu za Mulungu.

43 Ndipo ife tikudalira, lero, Mulungu, ngati alipo aliyense mkati muno omwe sali pamene iwo akuyenera kukhala, kapena sanamulandire Khristu panobe monga iwo akuyenera kuchitira, mulole ili likhale tsiku limene lachisavundi lawo, lingaliro Lamuyaya liti lipangidwe, kuti akakutumikireni Inu. Perekani izi, Atate.

44 Mulole Mkhristu aliyense, mkati muno, mulole mtima wawo utenthe mkati mwawo, kuti apite kunja kwinkwake, mmipanda ndi misewu, ndi kubweretsa miyoyo yotayika, ziribe kanthu momwe izo ziri zodzichepetsa, iwo akhoza kubweretsamo moyo umodzi umene ungapweretse millionsi kumbuyo kwake. Ife sitikudziwa zimene ife tikuchita. Nthawizina amayi aang'ono awa amadabwa, Ambuye, koma iwo samadziwa chimene iwo akuyankhula, pamene iwo akuyankhula kwa munthu wachichepere, kapena munthu wina wachikulire, kapena chinachake chokhudza moyo wawo. Perekani, Ambuye.

45 Tsopano lowani mu Mawu. Ambuye, Inu muli mu Mawu. Ndipo mutipatse ife chikhulupiriro kuti tiwapange Mawu kukhala amoyo ndi ochita, lero, mmiyoyo yathu, mu umunthu wathu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemelo Wake. Amen.

46 Ine sindikudziwa ngati anali Dwight Moody. Ine ndikukhulupirira anali, wokonza nsapato waku Boston, amene tsiku lina... Mkazi wamng'ono, mmasiku oyambirira a Methodisti, iye ankafuna kuwachitira Ambuye chinachake. Chotero, iye ankachapa, ndipo ankasunga ndalama zake, kuti apeze dola ndi theka, ine ndikukhulupirira, kuti mlaliki wakale abwere kudzamulalikira iye. Ndipo iye anali atabwereka khola, kwa kotala kapena chinachake, kwa usiku umenewo. Anakonza



kholalo, ndi kuyika—benchi yaying’ono yochapira pansi, ngati guwa.

47 Ndipo kuti ndikuwonetseni inu momwe izo ziriri zophweka, kwa inu amayi apakhomo, tsopano. Mukuona? Inu mukuti, “Oh, M’bale Branham, ngati ndingathe kulalikirira!” Inu simukuyenera kutero. Inu basi...Ndinu umboni. Ndinu chikoka; moyo wanu.

48 Ndipo iye anatenga timabukhu tina, ndipo anapita pakona, akulengezetsa msonkhano, ndi kumagawa ito. Nthawi iliyonse wina akagwira iko, iwo ankaponyera ito pansi. “Woyera-wodzigudubuza! Wotengeka!” Ndi kumapitirira. Mukuona?

49 Mnyamata wamng’ono wachikulire anabwera pafupi, ali ndi thalauza long’ambika. Andakoka a bambo ake anali pa mapewa ake; tsitsi likugwera pansi pa nkhope yake. Anati, “Dona, mukupereka chiyani?”

Anati, “Kabukhu, mwana.” Iye anapereka iko kwa iye, monga *choncho*. Iye anakayang’ana iko, anati, “Sindingathe kuwerenga.”

Anati, “Chabwino, kakuti kukhala msonkhano usikuuno, kumtunda kuno.” “Oh,” anati, “ukhalapo? Mudandaula ngati nditabwera?” Anati, “Iwe ukufuna? Iwe uyenera kubwera, wokondedwa, ngati ungate.” “Chabwino, ndichita zimenezo.”

50 Usiku umenewo, pambuyo pa kuyesetsa kwake konse, ndi kufooka. Mtumiki wakale wokhulupirika anabwera, anafika paguwa ndipo anapempherana. Anayimba nyimbo, iye ndi donayo, ndipo anakhala pansi ngati omvetsera ake.

51 Patapita kanthawi, akudzandima pa chitseko, anali mwana wamng’ono wosawoneka bwino uja, tsitsi likugwera pansi pa nkhope yake. Inu mukudziwa yemwe ameneyo anali? Dwight Moody. Usiku umenewo, iye anagwada pa guwa; anatomiza miyoyo milioni kwa Mulungu. Mukuona? Inu simukudziwa zomwe mukuchita.

Yankhulani mawu pang’ono kwa Yesu  
Chitirani umboni, yimbani, kapena  
pempherani,  
Ndipo monga mkate pa madzi  
Iwo udzabwerera kwa inu tsiku lina.

52 Izo nzoona. Chabwino. Ingokumbukirani, musalephere, musalephere; mupindulire miyoyo! Chirichonse chimene mungachite, muzipindulira miyoyo. Ine—ndine wokondwa kuwawona anthu athu pano, mmawa uno, palibe mmodzi wa iwo ali mu umphawi, monga ine ndikudziwira; nonse mwavala zovala zabwino, ndipo ndinu aukhondo; anthu owoneka anzeru. Ndine wothokoza kwambiri kwa Mulungu, kudziwa kuti inu muli mwanjira imeneyo.

<sup>53</sup> Ine ndinabwera kuno, amzanga, nthawi ina, mu kupsinjika, pamene ine ndinkalalikira nditavala ovololo. Ndipo inu munkayenda mamailosi, kudzafika kuno, ndipo munkawoloka dzikoli, ndipo mulibe zokwanira kuti mudyeye. Ndipo ine ndikudziwa. Uko nkulondola. Ine ndikukumbukira zimenezo. Mulungu watidalitsa ife, ndipo ndife oyamikira kwa Iye, mwaona.

<sup>54</sup> Koma mmawa uno, mwaona, momwe inu mukuwonekera mosiyana mmawa uno, ndine wothokoza chifukwa cha izo, koma musalole zimenezo zikuyimitseni inu. Kumbukirani kumene izo zikuchokera, kuchokera kumwamba. Ndipo, pindulani moyo, Uko umenewo udzakhala kwanthawizonse. Ndipo mwinamwake gawo lalikululu la inu mwina liri ndi akaunti yaku banki yaying'ono kwina kwake. Ndine wokondwa chifukwa cha zimenezo, ndipo Mulungu adalitse izo mochuluka. Koma musalole kuti zimenezo ziyime pa njira yanu ya kupindula moyo. Uko nkulondola. Muyambe kaye kusunga miyoyo.

<sup>55</sup> Tsopano ndimaganizira za mwinamwake... Ine ndinamufunsa M'bale Neville. Kapena, mulibe phunziro linalake la Sande sukulu, chotero ife timangophunzitsa kuchokera paliponse, ndi penapake mu Baibulo. Ndipo ndinaganiza za kuphunzitsa, mmawa uno, pamene ine ndinabwera kuno, ine ndisanabwere mchipinda, pafupifupi, pa Bukhu la Chivumbulutso.

<sup>56</sup> Kenako ndinakumbukira kuti purogramu ya pawalesi ili mkati—mndandanda wa Bukhu la Chivumbulutso. Charles Fuller, ndikuganiza, akupanga a—bukhu. Ndipo M'bale Fuller ndi wofanizitsa, iyemwini. Ndipo ine ndimaopa kuti ife tikhala ngati takhala pamodzi pa izo, ndipo inu munazimva kale zina za izo.

<sup>57</sup> Chotero, ndiye, ine ndinaganiza ife tipite ku Bukhu la Ahebri. Ndi labwino... Ndi angati amakonda Bukhu la Ahebri? Oh, ilo ndi lopambana... Tiyeni tipite ku mutu wa 10. Ine ndikuganiza umenewo ndi mutu wokongola. Ine sindikudziwa ngati ine ndinayamba ndaphunzitsapo pa iwo, koma mwinamwake ndinatero, kuno, gawo la iwo. Kawirikawiri ndimatenga ndime ziwiri kapena zitatu, ndiyeno izo zimakhazikitsa izo, ndipo ife timayamba mu Baibulo.

<sup>58</sup> Inu mukudziwa, nthawi ina, ndikadzabwera patchuthi, ndiri ndi njala yopezanso nthawi ina, imene ine ndidzakhoze kukhazikika pa kachisi, kapena kwina kwake kuno, ndi kudzangokhala ndi mndandanda wa maphunziro, monga ife tinkatengera Baibulo. Monga ngati pa Bukhu linalake, kungopita, kudzangolipesera ilo mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa m'Malemba monga chonchi. Izo zimayika ndi kukhazikitsa Chikhulupiriro chathu. Ndicho chimene maphunziro awa aliri, ndi kukhazikitsa Chikhulupiriro chathu.

<sup>59</sup> Tsopano, mu mutu wa 10 wa Ahebri. Ine sindikudziwa chifukwa chake, ndikungokhala mmenemo, ine ndinangotsegula iwo. Ndipo ife tikufuna kuti tiwerenge kuchokera apa, kwa phunziro laling'ono, ndi kuphunzitsa izo. Ngati tingafike pansi apa, tidzapeza kuti ife tinakhalamo kale mu zimenezo, ndiye ine ndi. . . titembukira ku chinthu china, kapena mwinamwake Ambuye atitsogolera ife ku chinthu china.

<sup>60</sup> Tsopano musaiwale misonkhano usikuuno pa kachisi pano. M'bale akhala akuyankhula kwa ife usikuuno. Ndipo ngati muli ndi abwenzi aliwonse kuzungulira New Albany kumusi kumeneko, kwa M'bale Matheny, ife tikayankhula kumeneko kanthawi pang'ono usikuuno. Ndipo kenako Lachitatu usiku.

<sup>61</sup> Ndipo M'bale Junior Jackson, ine ndinamumva iye akuti “ameni” kanthawi kapitako, koma sindinakanitise kuti ndimupeze iye. Ndipo iye ali mchipinda muno. Ndipo kwake ndi Lachinayi usiku, ndipo—ndipo ine ndikukhulupirira iye ali ndi Lamlungu usiku. Iwe uli pati, Junior? Ndikulephera kuti ndikupeze iwe. Oh, nzosadabwitsa; iwe wakhala kuseri kwa munthu wamkulu uyo kumbuyo uko. Wanu . . . Chani . . . Utumiki wako Lachisa- . . . Lamlungu usiku, nawonso, ndi choncho, Junior? [M'bale Jackson akuti, “Uko nkulondola.”—Mkonzi]. Lachinayi ndi Lamlungu. Chabwino. Ndipo misonkhano yake ili usikuuno, ndipo iye ali kunja pa State Street, mu New Albany. State ndi [“Monroe.”] Monroe.

<sup>62</sup> M'bale Genter, inu mukuona yakhala ili nthawi yayitali kuchokera pamene ine ndinkawerenga mamita, kapena kukonza ntchito iliyonse. Ine ndinaiwala misewu yonseyo. Koma pali a . . . Ine ndimawakondabe Ambuye Yesu omwewo amene anali ndi ife nthawi imeneyo, pamene ankandithandiza ine mmasiku amenewo.

<sup>63</sup> Ine ndimamuza m'bale, kanthawi kapitako. Ine ndinkakonda kupita kumusi kumeneko pamene ine ndinkawerenga mamita, ndi kugogoda pa chitseko. Kuwerenga mita, ndi kutulutsa Baibulo langa ndi kuwerenga kwa kanthawi, donayo asanafike pakhomo, chinachake chonga icho. Ndi kupeza nyumba yaing'ono yakale yopanda kanthu. Ndithudi, inu simungapeze izo tsopano, komwe winawake anasamukako. Kulowa mmenemo, ndi kukabwerera mu shedi ndi kugwada pansi ndi kupemphera. Uko kunali kupanga, icho chinali chinthu chimene chinakhazikitsa icho pamenepo, kuyang'ana kwa Iye.

<sup>64</sup> Tsopano, Bukhu la Ahebri ndi—kulekanitsa pakati pa lamulo ndi chisomo. Ndi angati amadziwa kuti ife timakhala moyo mwa chisomo, ndipo osati mwa lamulo? Ine ndikukhulupirira wolembayo. . . Palibe amene akudziwa ndendende. Koma izo ziri mochulukuka monga Paulo, mpaka

ine ndimakonda kuzitcha izo zolembe za Paulo. Ndipo iye ankayankhula kwa Ahebri.

<sup>65</sup> Tsopano, Uthenga anali utapita kale kwa Amitundu, chifukwa Ayuda anali atawukana Iwo. Ndipo iwo anali atapita kwa Amitundu ndi Uthenga. Ndipo tsopano Paulo ankalembanso kwa Ahebri, pakuti ambiri a iwo ankafuna kubwerera pansi pa lamulo, kusunga lamulo, ndipo nkumakhulupirabe mwa Khristu.

<sup>66</sup> Ndipo, inu mukudziwa, izo zikadalipo mpaka lero. Alipo anthu lero amene amayesetsa kusunga lamulo la Chipangano Chakale, ndi kukhalabe Mkhristu, pamene lina ndi lotsutsana kwambiri ndi limzake. Ngati iwe uchita gawo limodzi la lamulo, iwe ukuyenera kuchita lonse. “Iwe umadzakhala wangongole,” Baibulo limati, “tizichita lamulo lonse,” chotero, ngati uchita gawo lake. Ndipo, kenako, ngati musunga lamulo, monga nsembe, ndi masabata, ndi maudindo, ndi zakudya, ndi kutsuka, ndi zina zotero, pansi pa lamulo.

<sup>67</sup> Koma ife sitiri pansi pa lamulo tsopano. Ife tiri pansi pa chisomo. Ndipo Paulo akuyesetsa kuwonetsera pamene lamulo linali mthunzi. Tsopano, pachiyambi, apa ife tikuziwona zimenezo.

*Pakuti lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zirinkudza, ndipo osati chifaniziro chenicheni cha zinthuzo, sizingathe konse ndi nsembe zomwe iwo ankapereka chaka ndi chaka mosalekeza kumupanga wobwerayo kukhala wangwiro.*

<sup>68</sup> Oh, mai! Kodi zimenezo sizingapange ulaliki pamenepo? Mukuona? Mukuona? Tsopano, lamulo linali mthunzi wa zinthu zirinkudza.

<sup>69</sup> Tiyeni tifike apa, miniti yokha. Mutsegule ndi ine kubwerera ku . . . Ine ndikukhulupirira kuti ndi mutu 12 wa Chivumbulutso. Tiyeni tilowe mu zimenezo kamphindi chabe, ndipo tiwone ngati sitingathe kupeza chinachake chaching’ono chabwino pomwe pano, kuti tiyambirepo, kuganiza za “mthunzi.” Tsopano tiyeni—tiyeni tiwerenge kachiwiri, tsopano, inu ndi Baibulo lanu.

*Ndipo panawonekera chozizwa chachikulu m’mwamba; mkazi . . .*

<sup>70</sup> Kodi *mkazi* amayimira chiyani mu Baibulo? Mpingo.

*. . . mkazi atavekedwa ndi dzuwa, (chimenecho chinali chovala chake chimene iye anali atavala, mwaona), ndi mwezi pansi pa mapazi ake, ndi pamutu pake korona ndi nyenyezi thwelofu:*

*Ndipo iye pokhala woyembekezera anafuula, mu zowawa za kubala, ndi kumva zowawa zakubala.*

<sup>71</sup> Zindikirani, mkazi anawonekera mu mlengalenga, ku a—masomphenya a Yohane mvumbulutsi. Ndipo a . . . Iye

anavekedwa ndi dzuwa. Ndipo mwezi unali pansi pa mapazi ake. Ndipo anali ndi nyenyezi thwelofu mu korona wake.

<sup>72</sup> Tsopano kodi zimenezo zikuimira chiyani? Masomphenya ndi ziphiphiritso. Tsopano, mkazi ndi mpingo. Ndipo mpingo unali. . . Mwezi unali pansi pa mapazi ake. Mwa kuyankhula kwina, iwo unkawalabe, koma iye anali pamwamba pake. Chifukwa, iye anali atakhala kale mu chikhalidwe chakuti iye ankabala mwana. Iye ankamva ululu mu kubala. Ndipo mwezi unkapita, ndipo dzuwa linkawala. Tsopano, mwezi ndi. . .

<sup>73</sup> Nchiyani chimene chimapangitsa mwezi kuwala, ndi dzuwa likuwalira pa iwo. Ilo ndi mthunzi chabe wa dzuwa. Ndipo, chotero, mwezi unali utakhala tsiku lake, ndipo dzuwa linali likutuluka. Mkaziyo anali asanavekedwe mwezi. Iye anavekedwa dzuwa; iwo unali mpingo wa Uthenga ukubwera mu kukhalapo. Mpingo wakale wa Orthodox. . .

Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, kodi umenewo unali Orthodox?” Inde.

<sup>74</sup> Yesu anadza koyamba kwa Myuda, osati Wamitundu. Mukuona? Iye, Iye anawalamulira ophunzira Ake kuti asapite kwa Wamitundu aliyense. Iye anati, “Iye anabwera kwa Ake omwe, ndipo Ake omwe sanamulandire Iye.” Chiyani? Iye ananena, pamene Iye ankawalamulira iwo, mu mutu wa 10 wa Mateyu Woyera. Iye anati, “Musapite mu njira ya Amitundu, koma makamaka mupite kwa nkhoa zotayika za Israeli. Ndipo pamene mukupita, muzikalalikira, kumakati Ufumu wa Kumwamba wayandikira.” Mukuona? “Musapite mnjira za mzinda wa Samariya, kapena zina za njirayo, koma muyambe mwapita kwa nkhoa zotayika za Israeli.”

<sup>75</sup> Ndi chifukwa chake kuwala kwa dzuwa kwa ulemelero kunkawala mozungulira mkaziyo. Ndipo iye, pokhala mu zowawa, akuvutika, kuti abeleke Mwana uyu.

*Ndipo anabala mwana wamwamuna, amene akanati adzalamulire mitundu yonse ndi ndodo yachitsulo: . . .*

*. . . ndipo chinjoka chinayima pambali pa mkaziyo chimene chinali (Roma) kuti chikamulikhwire mwanayo mwamsanga pamene iye abadwa.*

<sup>76</sup> Ndipo Roma anamuzunzadi Mwanayo. Iwo anatumiza ndipo anakapha ana onse, kuyambira usinkhu wa zaka ziwiri kumakwera mmwamba. . . kapena, zaka ziwiri kumatsika pansi, kani, kuti iwo akathe kumupha Khristu, ndi kumugwira Iye mmenemo. Herode anayambitsa nkhaniyi.

*. . . koma mwana wa mkaziyo anakwatulidwira kwa Mulungu, . . .*

<sup>77</sup> Kuchokera ku chiwukitsiro, “anakwatulidwira kwa Mulungu, ndipo akukhala pa dzanja lamanja la Mulungu.”

Tsopano, izo zingangodula chiphunzitso cha “mwana wamwamuna” chonse, sichoncho izo? Mukuona?

<sup>78</sup> Koma tsopano, “Lamulo,” Ahebri 10 kachiwiri, “pokhala nawo mthunzi wa zinthu zirinkudza,” ndipo osati fanizo lomwelo, koma mthunzi.

<sup>79</sup> Tsopano, usiku wina, ine ndinali kukambirana ndi munthu wabwino kwambiri, pa chiphunzitso cha Zakachikwi. Ine ndinati, “Ine ndimakhulupirira mu Zakachikwi, chifukwa pali mithunzi yochulukira kwambiri ya Chipangano Chakale izo zimayankhula kuti padzakhala Zakachikwi. Pakuyenera kukhala. Mithunzi yambiri!”

Iwo anati, “Kodi Mpingo udzadutsa mu Chisautso?”

<sup>80</sup> Ine ndinati, “Ayi. Mpingo sungadutse mu Chisautso, Iwo ukuyenera kupita Chisautso chisanafike. Mithunzi yambiri!” Penyani, kuti, Nowa, pachiyambi, Nowa... “Chipangano Chakale chonse, lamulo lonse, tsopano, linali mthunzi wa zinthu zabwino zirinkudza.”

<sup>81</sup> Tsopano, nthawi ya chisautso isanafike, choyamba, Enoki, a... Nowa, Nowa anali choyimira cha amene anatengedwa, monga namwali wogona, koma Enoki anasandulika chisautso chisanafike. “Ndipo Enoki anatengedwera mmwamba, ndipo sanapezekenso, chifukwa Mulungu anamutenga iye,” choyimira cha kupita kwa Mpingo. Ndipo Nowa anamuwona iye. Pamene anamuwona Enoki akupita, iye anadziwa kuti inali nthawi yoti alowe mu chombo, kuti anyamulidwire kudutsa mu chisautso.

<sup>82</sup> Baibulo linati, “Panali anamwali khumi anapita kukakumana ndi Mkwati; ndipo asanu anali ochenjera, asanu anali opusa. Ndipo iwo onse anali anamwali, aliyense wa iwo. Koma asanu anali ochenjera, ndipo iwo anali ndi Mafuta mu nyali zawo. Ndipo iwo anatuluka kukakomana ndi Mkwati. Ndipo Mkwati anabwera, ndipo iwo amene anali ndi Mafuta analowa.” Mwaona, kusandulika, kupita ndi Mkwati.

<sup>83</sup> Koma iwo amene anasiyidwa mmbuyo, iwo anabwera ndipo ankafuna kulowa, nawonso. Chimodzimidzi monga iwo amene anabwera ndi kudzagogoda pa khomo la chombo, “Nowa, tilowetse ife,” koma Mulungu anatseka chitsekocho.

<sup>84</sup> Ndipo, oh, mzanga wa ine, limodzi la masiku awa, Mulungu adzakupatsa iwe kuyitana kwako komaliza. Kenako chitseko chidzatsekedwa, pakati pa chifundo ndi chiweruzo. Usadzasiyidwe kunja. Lowa mkati tsopano pamene iwe ungate. Usapereke chidwi ku zomwe dziko likunena. Lowa mwa Khristu. “Pakuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi ndi Iye.” Mukuona?

Kenako, namwali wochenjera uyu anapita, mu kusandulika.

<sup>85</sup> Ndipo enawa amene anabwera ndi kudzagogoda pakhomo, chinachitika ndi chiyani? Chinachitika ndi chiyani? Baibulo

linati, “Two anaponyedwa mumdima wakunja, kumene kunali kulira ndi kusisima ndi kukukuta kwa mano.”

<sup>86</sup> Israeli, pamene nthawi ya chisautso inakantha Igupto, panalibe chinthu chimodzi chomwe chinakantha Igupto... Aisraeli, chifukwa iwo anali mmalo operekedwa ndi Mulungu, Gosheni. Kunalibe zisautso nkomwe. Mukuona? Ena onse a iwo anali mu chisautso, koma osati uyu.

<sup>87</sup> Tsopano, zinthu zonsezo pokhala mithunzi, izo zikuyenera kuyimira chinachake. Ndiyeno pamene ife tikuwoneratu kudza kwa Ambuye, ife tikuwona momwe anthu ankayendera mmasiku amenewo, ndi kuwona momwe anthu ankakhalira. “Aliwuma, odzikuza, okonda zosangalatsa kuposa okonda Mulungu.” Umo ndi momwe ziliri lero. Amuna akuyenda motsatira zilakolako zawo zoipa. Izo zafika ku chinthucho... Mukhululuke kufotokoza uku, alongo anga. Koma izo zafika, mpaka, makhalidwe abwino enieni ndi chinthu chakale, pakati pa anthu athu.

<sup>88</sup> Dzulo, mu Chipatala cha Saint Edwards, ine ndinamumva dokotala akumukhadzulira mtsikana wina mzidutswa kumbuyo uko. Iye anakwera pa masitepe omwe ine ndikanakhoza kugwira dzanja lake, aliyense mchipatala anali akumvetsera, akuyang’ana. Uko kunali mtsikana kumbuyo uko, atavala zina zazing’ono izi, zovala zachikale zopanda umulungu, ngati akabudula aang’ono.

<sup>89</sup> Inu mukudziwa chimene Baibulo limanena za izo? Iye amati, “Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu, kuti mkazi azivala thalauza ngati mwamuna.” Kulondola.

<sup>90</sup> Ndipo apo iye anali, akuye...Dokotala anati... Munthu wamng’ono, wolumala. Ine ndikumudziwa iye, koma ndikulephera kuganizira dzina lake. Iye anati, “Mukutanthauza kundiuza ine kuti asisitere anakulolani inu kuti mulowe mchipatala muno monga choncho?” Anati, “Bwanji, ndinu chamanyazi ku chipatala. Chokani muno.”

Ine ndinati, “Mnyamata, ndikufuna ndikugwire chanza.” Ndithudi.

<sup>91</sup> Anati, “Munafikako bwanji kutsogolo? Kodi inu simukuchita manyazi ndi inueni, kubwera muno mutavala monga choncho?”

<sup>92</sup> Ine ndinaganiza, “Oh, m’bale, izo nzoona.” Ndimasilira mwamuna wolimba mtima mokwanira kuti azitcha chabwino “chabwino,” ndi cholakwika “cholakwika,” mosalabadira chimene iye ali. Mukuona? Koma, chinthu chaulemu, oh, ine ndingakhoze... .

<sup>93</sup> Inu mundikhululukira ine, sichoncho inu? Ine ndikufuna ndiyime apa miniti yokha. Tsopano, ine ndikufuna, ndikhoza kuziwongola izi pang’ono chabe, mzanga wokonededwa.

Musaganize kuti M'bale Branham akuyesera kukhala wamwano. Ine sindikutero. Ine ndikungoyesera kunena choonadi. Ndipo chimene ine ndikudziwa, kuti uko mu Ulemelero, tsiku lina, ngati ine ndidzawone moyo wanu uli ndi mwaye, ndiyeno ine nkudziwa kuti ine ndinali amene ndinapangitsa zimenezo, ndipo kumadziwa Choonadi ndipo osachinena Icho. Ayi, ine ndichotsa izo pa mapewa anga, kupita pa anuwo. Inu mupange chigamulo chanu.

<sup>94</sup> Akazi athu amene amavala monga choncho, ali ndi mzimu woyipa. Mukuona? Pali chinthu chimodzi chokha mu Lemba chimene chinachita zimenezo. Ameneyo anali mdierekezi, anawavula anthu. Penyani. Tsopano, ine sindikutanthauza kunena kuti ndinu wachigololo; ine sindikutanthauza zimenezo, mlongo wanga wokondedwa. Koma inu muli mumayendedwe atsikuli, mwanjira imeneyo, mpaka inu mophweka basi... Mumaganiza kuti ndi zabwino chifukwa ena amachita zimenezo, ndipo inu simuzindikira kuti ameneyo ndi mdierekezi akuchita zimenezo. Ndithudi, ndi iyeyo. Sindinu wotchuka ayi. Ndinu wopenga. Pepani kafotokozedweko. Chabwino, uko nkulondola. Ine ndikutanthauza, mukupengera chinthucho kutali ndi Mulungu.

<sup>95</sup> Oh, Mzimu Woyera wa Mulungu, si nthawizonse umalimbana ndi munthu. "Sakufuna kuti aliyense awonongeke, koma kuti onse afike ku kulapa." Ndipo Mulungu atipatse ife kulimbika, mu tsiku limene alaliki... Apa ndi pamene izo zinayambira, ndi chifukwa chakuti abusa anu, pa nsanja, amapirira nazo izo. Izo nzoona. Inu mukuyenera kuti muchotsedwe. Ngati ine ndikanakhala ndi mpingo, ndipo akazi nkumachita zimenezo mu tchalitchi, nthawi yomweyo iwo angachoke mu bukhu la mpingo. Inde, bwana. Pomwepo, mpaka mutawongoka, kuyamba molondola. Mulungu awayimbe mlandu. Koma, lero...

<sup>96</sup> Ine ndinapita ku Saint Joseph. Kawirikawiri ine ndimakhala pa mafoni akuchipatala awa, zadzidzidzi izi. Ndinapita kunja uko kuti ndikamuwone mwana wamng'ono, akufa, khansa... kapena vuto la impsyo; anachotsa impsyo imodzi, masiku awiri kapena atatu okha. Ndipo momwe kuti mwana wamng'ono wosaukayo... Ndipo pamenepo ine ndinazindikira, mu chipatala cha Chikatolika, abwino kwambiri ndi opereka.

<sup>97</sup> Ndinapita ku chipatala cha Chiprotestanti. Kunali dona amene amamwalira, ndipo ndinapita kuti ndikayike manja anga. Wopempheretsa, atayima pamenepo, anati... Ndipo ine ndinamudziwitsa iye kuti ine ndinali wachipembedzo chomwecho chimene iye anali nacho. Anati, "Huh! Ayi! Musatero, musatero, musatero! Musachite zimenezo. Musayike dzanja lanu pa iye."

Ine ndinati, "Baibulo linatero."



<sup>98</sup> “Ah, tulukani!” Anati, “Zinthu zimenezo si zabwino. Ayi, ife sitikufuna kuti inu muyike manja anu pa munthu wodwalayu mkati muno.” Mukuona momwe izo zimakhallira?

<sup>99</sup> Ndipo ndi chifukwa chake mpingo wa Katolika ukuwameza iwo, mwa masauzande. Uko nkulondola. Chifukwa, Achiprotestanti sanapite mwakuya mokwanira mwa Mulungu kuti akhale ndi chowachitikira, kuti adziwe chimene chipulumutso chenicheni, chanthawi yakale, chokhudza mtima, Mphamvu ya Mulungu, chiri. Ndi limenelo gulu lanu lapakati. Ndi limenelo gulu lanu lodzazidwa, likuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Ameni. Ndi zimenezotu.

<sup>100</sup> Zindikirani, “Lamulo kukhala ndi mthunzi.” Zinthu zonsezi zimene ife tikuziwona tsopano ndi mthunzi, zinali mithunzi, ndipo tsopano izo zikusanduka zenizeni. Chimodzimodzi monga mtengo ukuphukira, ndipo iwo umadzasanduka nthambi; kenako iyo imapita ku mbewu, kuti ikabale mbewu ya mtundu womwewo imene inalowa mu nthaka. Zinthu zonsezi zimachokera mu Genesis. Ndipo, lero, tsopano . . .

<sup>101</sup> “Koma opembedza awa, amene anabwera pansu pa mthunzi, sakanatha kupangidwa angwiro.” Tiyeni tikhazikike pa mawu amenewo pamene.

*. . . iwo ankapereka chaka ndi chaka mosalekeza  
kupangitsa wakudzayo kukhala wangwiro.*

<sup>102</sup> Ine ndikufuna kuti inu tsopano . . . Kodi simunamve, nthawi zambiri, anthu amati, “Oh, palibe mmodzi wangwiro”? Uko nkulondola, simungakhale wangwiro pamaso pa munthu mzanu.

<sup>103</sup> Koma inu mukuyenera kukhala wangwiro, kapena inu simudzapita konse Kumwamba. Kulondola. Baibulo linati, Yesu akuyankhula, mu chiphunzitso cha paphiri, Mateyu; anati, “Khalani inu chotero angwiro, monga Atate anu a Kumwamba ali wangwiro.” Ndiye, inu mukuyenera kungokhala wangwiro monga Mulungu ali, kapena inu mwatayika. Tsopano inu mudzachita motani zimenezo? Mukuona?

<sup>104</sup> Tsopano, kulakwitsa kumodzi kwakung’ono, ndipo inu mwatayika; kutsutsa kumodzi kwakung’ono kwa diso, ndipo inu mwapita; chifukwa palibe chimene chingalowe mu Malo amenewo koma “changwiro.” Mulungu anamuyika Satana Kumeneko, nthawi ina, ngati Mngelo, chimene iye anali Mwana wa Mmawa, ndipo iye anatenga zinthu zabwino za Mulungu ndipo anazipotoza izo kukhala zoyipa. Mulungu ndi wotsimikiza kuti palibe chimene chidzalowe Mmenemo chimene chidzachite konse zimenezo. Mukuona?

<sup>105</sup> Tsopano, inu mukuyenera kukhala wangwiro. Yesu anati, “Chotero khalani inu angwiro, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali wangwiro.” Tsopano, zidzatheka bwanji kuti mudzakhale, pamene inu mukuchimwa mopitirira, pamene inu mopitirira mukuchita chimene chiri cholakwika? Tsopano,

ichi chikhala ngati chiika chosokoneza pang'ono mwa achilamulo, koma, zindikirani. Si zimene inu mumachita; ndi zimene Mulungu wachita. Si zimene inu mumachita; ndi zimene Iye anachita. Mukuona? Inu simungakhale angwiro; inu simungakhale, mwa inueni. Koma, mwa Khristu, inu mumakhala angwiro. Inu simukudalira ntchito zanu zabwino, kapena mpingo wanu womwe umene inu mulimo, koma inu mukudalira mu Magazi okhetsedwa a Ambuye Yesu. Ndi zimenezotu. Icho ndi chimene chimakupangani inu kukhala wangwiro. Icho ndi chimene chimazika chikhulupiriro chanu.

<sup>106</sup> Kenako, pa machiritso Auzimu, mwanjira yomweyo. Sindikudalira momwe ine ndikumverera. Ngati nditatero, ine ndingakakhale pa bedi, mmawa uno. Koma ine ndikudalira pa ntchito Yake yotsirizidwa. Iye ananena izo; Iye analonjeza izo; ine ndikukhulupirira izo. Mukuona? Ndi zimenezotu. “Chotero khalani inu angwiro.”

<sup>107</sup> Tsopano, oh, mulole ife tingotenga pang'ono pokha mbali imodzi, chinachake chagudubuzidwira mu mtima mwanga. Ndiloleni ine ndikufunsemi inu chinachake. Ife tikukhala mu tsiku la chiweruzo tsopano, osati Chiweruzo chachikulu, koma kuyitanidwa kutuluka kwa Mpingo. Inu mukukhulupirira zimenezo? Tikukhala mmasiku a tsankho. Pali a—tsoka, a—kusankhana mitundu kukuyesera kuchuluka mdziko. Izo ndi zamkutu. Koma ilipo nthawi yeniyeni ya tsankho; chabwino kwa choipa. Mulungu amawalekanitsa anthu Ake, amawaitanira iwo atuluke. Kodi inu mukudziwa, mawu kumene akuti *mpingo* amatanthauza “kusankhidwa; oyitanidwa atuluke; kulekanitsidwa”? Amen. “Tulukani pakati pawo,” Baibulo limatero, “musakhale otengapo nawo gawo mu tchimo lawo ndi chidetso chawo, ndipo ine ndidzakulandirani inu kwa Inemwini. Ndipo inu mudzakhala ana aamuna ndi aakazi kwa Ine, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu kwa inu. Tulukani!” Ndi nthawi yolekanitsa. “Ndipo mochuluka pamene inu mukuona tsiku ili likuyandikira.”

<sup>108</sup> Mpingo umene nthawi ina unkayesera kuyenda, iwo anadzipanga okha chipembedzo, ndipo tsopano iwo akudzakhala mu chisokonezeko chimodzi chachikulu kwambiri chokhala ngati dziko. Mwaona, monga momwe Baibulo linanenera kuti iwo anachita mu Chipangano Chakale, chomwechonso iwo adzatero, ambiri a iwo. Mulungu anawayitana iwo, anawawonetsera iwo zozizwitsa ndi zodabwitsa, ndipo m'badwo wonse unawonongeka mchipululu; iwo atatha kuwona zozizwitsa, Mulungu atatha kuchita zozizwitsa pa iwo, iwo atatha kuwona ulemelero wa Mulungu. Koma, mu mtima mwawo, iwo anali osakhulupirira, ong'ung'udza kwa Mulungu, odandaula. Mulungu anangoti, “Dzipatule wekha, Mose.” Ndipo Iye anayambitsa m'badwo watsopano, kuti awatengere iwo ku dziko lolonjezedwa.

109 Zindikirani. Ndi angati muno mmawa uno ali Akhristu? Kodi mungakweze manja anu, ingokwezani manja anu mmwamba, “Ndine Mkhristu.” Mulungu alemekezeke, kuti ndinu Mkhristu. Munadzakhala chotani Akhristu? Chifukwa Inu munati, “Ine—ine ndikufuna kukhala Mkhristu?” Chifukwa chakuti inu munkamfunafuna Mulungu, ndi misozi? Chifukwa Mulungu, mwa chisomo, anakuyitanani inu. Uko nkulondola. Osati chifukwa munkamfunafuna Iye; chifukwa Iye ankakufunafunani inu.

110 Tsopano, ngati inu mungazindikire, ku mbali ya Baptisti, kapena Chipresbateria, chikhulupiriro cha Arminian, iwo onse amapita ku mbewu. Iwo amati, “Chabwino, ngati Mulungu anandiyitana ine, aeluya, ndiye ine ndiri bwino. Ndizichita zimene ndikufuna.” Izi zikusonyeza kuti mulibe icho, ndipo simunaitanidwe. Uko nkulondola. Ngati Mulungu anakuitanani inu, inu mudzamukonda Iye mwaumulungu, zinthu za mdziko zidzakhala zakufa kwa inu. Uko nkulondola.

111 Mnyamata wakhala kumbuyo uko akujambula tsopano. Iye anandifunsa ine, akubwera, amene ali wanga. . . mmodzi wa abale anga, Bambo Mercier. Ndipo amajambula Mauthenga mmisonkhano, ndi mzake; Leo ndi—ndi Gene, kumbuyo kuno. Leo anati kwa ine, akubwera mmawa uno, iye anati, “M’bale Branham, chinali choyamba ndi chiyani; chikhulupiriro chimabala chikondi, kapena chikondi chimabala chikhulupiriro?”

112 Ine ndinati, “Chikondi chimabala chikhulupiriro. Osati chikhulupiriro, chikondi. Iwe umayenera uzikonda, poyamba, iwe usanakhale ndi chikhulupiriro.”

113 Chotero, ngati inu mutanena kuti muli ndi chikhulupiriro, ndipo osamukonda Mulungu mwaumulungu, chikhulupiriro chanucho ndi chachabe. Mukuona? Mukuyenera muzimukonda Mulungu. Chotero, mukhoza kujowina mipingo yonse mdziko, kuchita chirichonse chimene inu mumafuna kuchita, kupanga kuvomereza konse kumene inu mukufuna; koma ngati palibe chikondi chenicheni, chenicheni, cha Mzimu Woyera, chobadwa mwatsopano mu mtima mwanu kwa Mulungu, chikhulupiriro chanu ndi chachabe. Ziribe kanthu mochuluka momwe inu mumavomereza kuti mumamukhulupirira Mulungu, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Izo zikuyenera kubadwa mu mtima wa munthu, mukatero inu mukhala ndi Moyo Wamuyaya, simungalekanitsidwe ndi Mulungu.

114 Tsopano, ngati ife tikanakhala ndi nthawi, powona kuti palibe ambiri a inu muli ndi Mabaibulo, koma mu Bukhu la Chivumbulutso. Mvetserani tsopano. Valani chipewa chanu choganizira, ndipo tsegulani mtima wanu. Ine ndikufuna kuti ndinene chinachake apa tsopano. Ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwatcheru, pamene Mzimu Woyera uli pafupi.

115 Baibulo linanena, mu Chivumbulutso, kuti, wotsutsakhristu akanadzabwera mu tsiku lotsiriza, ndipo kuti iye adzakhala wamwano kwambiri. Ndipo mu Mateyu Woyera, aponso, mutu wa 24, Yesu akuyankhula, anati, “Pamene wotsutsakhristu adzabwera, kuti iye—iye adzakhala wapafupi kwambiri, monga ntchito yeniyeni ya Mulungu, mpaka iye akanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheka.” Penyani, “Kunyenga Osankhidwa omwe. . .”

116 “Osankhidwa,” izo zikuchokera kuti? Kuchokera ku mawu akuti “Kusankhidwa.” “Iye akanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.” Mukuona? Koma si choncho. Mulungu alemekezeke chifukwa cha zimenezo! Izo sizingatheke.

117 Monga uko mu Ahebri, mutu wa 6, Iye anati, “Pakuti ndi zosatheka kwa iwo amene anawunikiridwapo kale, ndipo apangidwa kukhala otenga nawo Mzimu Woyera, ndipo analawa mphatso zakumwamba, ndi mphamvu ya dziko lirinkudza, ngati iwo atatembenuka ndi kudzikonza okha mu kulapa.” Izo ndi zosatheka. Izo sizingachitike. Uko nkulondola. Izo zikhoza kutsanziridwa. Izo zikhoza kunyengezedwa. Anthu akhoza kuchita ngati *wakuti-ndi-wakuti*, ndipo akhoza kutengeka ndi kanthu kakang’ono kalikonse.

118 Koma munthu amene anabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, yake—njira yake yalunjika ku Nyenyezi ya Kumpoto. Aleluya! Ndipo gehena yense sidzamugwedeza konse iye. Uko nkulondola. Ine sindikunena kuti iye sadzalakwitsa. Ine sindinganene kuti iye sangaterereke ndi kugwa. Uko nkulondola. Koma mwamsanga pamene iye angathe kudzuka pamapazi ake kenanso, maso ake amakhala ali pa Nyenyezi uko, ndipo iye amasunthira chitsogolo. Ndithudi. “Osankhidwa!”

119 Tsopano, Baibulo linati, ndipo ine ndikudziwa kuti awo ndi Mawu a Mulungu wamoyo. Baibulo linanena izi. Mvetserani tsopano. Mukuona? “Ndipo chirombo, ndi mneneri wonyenga,” m-n-e-n-e-r-i, mmodzi. “Ndipo chirombo,” mphamvu. Utatu wa gehena; monga ngati utatu wa Mulungu. Tsopano penyani.

*Ndipo iye anapangitsa onse, onse aang’ono . . . aakulu, amene ali olemera kapena osauka, kapolo kapena mfulu, (mwamuna kapena mkazi, mwamuna kapena mkazi, mwana kapena aliyense amene anali) . . .*

*. . . iye anapangitsa onse, awiri onse aang’ono ndi aakulu . . . kulandira chizindikiro mu yawo . . . mphumi, ndipo anasindikizidwa kulowa mu ufumu wa mdima.*

120 Tsopano pali zisindikizo ziwiri zomwe zikuchitika lero. Ndipo inu simukudziwa basi nthawi yanji. . . Oh, m’bale, mulole izi zipite pansu mwakuya. Inu simukudziwa kuti ndi nthawi yanji, imene inu amene muli mmalire lero, mupange lingaliro lanu lomaliza. Uko nkulondola. Inu simungagwedezeke motalika kwambiri. “Mzimu wanga sudzalimbana nthawizonse

ndi munthu.” Chotero, inu mukhoza kugwedezeke kwa kanthawi. Koma, “Mzimu wanga sudzalimbana ndi munthu nthawizonse,” pokhala mmalire.

<sup>121</sup> Zindikirani, chilemba cha chirombo ndi chilemba cha chinyengo, mdierekezi, ntchito za mdierekezi. Yesu anati, “Ndi umembala wawo wa mpingo”? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. “Mwa zaumulungu zawo”? [“Ayi.”] “Mwa chowachitikira chawo chaku seminare”? [“Ayi.”] “Ndi *chipatso* chawo inu mudzawadziwa iwo.”

<sup>122</sup> Tsopano, chotero, chipatso cha Mzimu Woyera ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, ubwino, kudekha, chipiriro, chifatso. Ichu ndi chipatso cha Mzimu. Ndipo, chipatso, ndicho chilemba cha Mzimu Woyera, kuwonetsera kuti chikondi Chauzimu chazikika mu mtima, ndipo zinthu za mdziko ndi zakufa.

<sup>123</sup> Tsopano, chilemba cha mdierekezi, ndi kutsanzira; ntchito, osati chisomo. Ntchitozo zimachitira mthunzi zinthu zimene zirinkudza; chinyengo, kupita ku tchalitchi, kunamizira kukhala Mkhristu; kumakhala monga dziko, kumakhala ndi zochita ndi dziko, kumapita kunjira ndi kumakachita monga dziko. “Ndipo zoyandikana kwambiri,” mpaka mbali ziwiri zonse zidzidzawoneka chimodzimidzi, “kudzanyenga Osankhidwa omwe. . .” Apa pali membala wa mpingo, amapita ku tchalitchi nthawizonse; munthu wabwino kwambiri, amapita ku tchalitchi; munthu wabwino, wamakhalidwe abwino. Koma, komabe, pansu mu kuya kwa umunthu wawo wamkati, palibe chochitika cha kukhalapo kwa Yesu.

<sup>124</sup> Tayang’anani pa Esau ndi Yakobo. Bwanji, Esau anali munthu wabwino pawiri kuposa Yakobo. Ndithudi, iye anali. Koma, Yakobo anali ndi chinthu chimodzi, “Iye anali ndi chobwezera ku mphotho.” Iye anawona ufulu wakubadwa umenewo, ndipo anawuwerengera iwo kukhala chinthu chachikulu kwambiri pa dziko lapansi.

<sup>125</sup> Ndipo, lero, ife timayesetsa kuwerengera kupita ku tchalitchi, kukamumva Dr. *Wakuti-ndi-wakuti* kapena M’bale *Wakuti-ndi-wakuti* akuyankhula, kumachita zinthu monga zimenezo, kapena kujowina mpingo wabwino ndi gulu labwino kumapitirira, chitsitsimutso chabwino. Ife timazitcha zimenezo kuchita chinachake chabwino. Izo si choncho.

<sup>126</sup> Mulungu amayang’ana pa mtima. Ndipo, mtima wa Yakobo, sunasamale chimene chimabwera kapena kupita. Panali cholinga chimodzi chokhazikika kwa iye, ndicho, kuti akatenge ufulu wakubadwa umenewo.

<sup>127</sup> Alipo wokhulupirira weniweni, lero. Siyani dziko likutcheni inu chirichonse chimene iwo akufuna. Asiyeni iwo anene kuti ndinu wotengeka, ngati iwo akufuna kutero. Iwo anamutcha Yesu, “Belezebule.” “Ndi mochulukuka bwanji momwe iwo

adzakutchuleni inu,” Iye anatero. “Odala ndi inu pamene anthu adzakuzunzani inu, kudzanena mtundu wonse wa choipa motsutsa inu, monama, chifukwa cha Ine. Sangalalani, ndipo mukhale okondwa mochulukwa, chifukwa mphototho yanu ndi yaikulu Kumwamba, pakuti motero iwo anazunza aneneri apambuyo panu.” Inu mukuona zimenezo?

<sup>128</sup> Tsopano, kodi Chisindikizo cha Mulungu ndi chiyani, ndiye? Aefeso 4:30, anati, “Musakhumudwitse Mzimu Woyera.” Chiyani? Aefeso 4:30, inu amene mukulemba zimenezo. “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera.” Tsopano, ine ndikudziwa ena a iwo amati ndi *ichi*, kapena *icho*, kapena *chinacho*. Koma, ziribe kanthu, Baibulo linati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona.”

<sup>129</sup> Ena amati, “Kusunga masiku, ndi chizindikiro.” Ndipo ena amati, “Kuchita *ichi*, ndi chizindikiro.” Ndipo ena amati, “Kukhala mboni ya *ichi*, ndi chizindikiro.”

<sup>130</sup> Koma, Baibulo linati, “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka Tsiku la mawomboledwe anu.” Mpaka liti? “Kufikira Tsiku la chiwombolo chanu.” Izo zingachitidwe motani?

<sup>131</sup> Kodi Mulungu angalakwitse? Kodi Iye angamupatse munthu Mzimu Woyera. . . Ndipo Iye pokhala wopandamalire, amadziwa kuchokera kuchiyambi mpaka kumapeto, kodi angamupatse munthu Mzimu Woyera, ndi kumulonjeza iye Moyo Wamuyaya, ndipo kenako nkudzatembenuka, kuwuchotsa Iwo kwa iye? Izo zingamupange Iye kukhala wamalire, monga ine ndi inu, wokhoza kulakwitsa.

<sup>132</sup> Koma, mathokozi akhale kwa Mulungu, Atate athu Akumwamba samalakwitsa. Iye. . . Ndithudi. Iye sangapange kulakwitsa. Kuyambira pachiyambi, Iye anali wopandamalire; ndipo Iye adzakhala, pa mapeto. Iye sangalakwitse. Iye ndi wangwiro.

<sup>133</sup> Zindikirani, tsopano ndikubwerera mu—mu Ahebri kachiwiri. Tsopano, “Khalani inu angwiro.” Tsopano ndilumphatse tsopano ndipita ku Chivumbulutso.

*Ndipo iye anapangitsa onse, awiri onse. . . aakulu, (aakulu, aang’ono, mwamuna ndi mkazi) . . . kapolo ndi mfulu, kulandira chizindikiro pamphumi pawo, ndi mu dzanja lawo:*

<sup>134</sup> “Ndipo iye anawanyenga onse kupatula iwo amene mayina awo analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.” Iye anawanyenga onse, dziko lapansi lonse, magulu achipembedzo. Iye analandira Mkhristu wonyengezera. Iye ananyenga membala wa mpingo. Iye ananyenga munthu wamakhalidwe abwino. Iye ananyenga munthu wabwino. Iye ananyenga wotchedwa mlaliki. Iye ananyenga wotchedwa Mkhristu.

135 Iye ananyenga onse ndi mabodza ake aakulu, akuti, “Ife tonse ndi mpingo umodzi waukulu, ndipo tonse tikuyenera kugwirizana pamodzi, ndipo anapangitsa zinthu za mdziko ndi mpingo ndi boma, kulumikizana. Chimene icho . . . Tithetsa nkondo zonse, kwanthawizonse.”

136 Amayi masauzande, mamillioni a iwo, adzati, “Icho ndi chinthu chimene ife tikufuna.” Penyani kumene izo zikuchokera, mlongo. Penyani kumene maziko ake ali.

137 “Ndipo iye ananyenga onse amene mayina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.”

138 Tsopano kodi inu mwakonzeka? Ndi ichi apa. Ndi mipope ya mfuti ya pawiri ndiponso yolongezedwa mwamphamvu. Mvetserani kwa zimenezo, tsopano. “Iye ananyenga onse amene mayina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa . . .” Kuyambira nthawi imene iwo anajowina mpingo? Kuyambira nthawi ya chitsitsimutso? Mayina awo analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa pamene iwo anabwera mu tchalitchi? Ayi. “Mayina analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuyambira maziko a dziko lapansi!” Ameni. Izo zimachita zimenezo. Inu mukumvetsa izo? Zimenezo zakhala zikulambalalidwa, kwa zaka mahandirede, pakati pa aziphunzitsi.

139 Koma, taonani, dzina la Mkhristu silinalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa pamene iye anabwera paguwa. Baibulo linati, “Dzina lake linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, njira yonse kuchokera ku maziko a dziko lapansi.” “Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye. Ndipo yense amene adza, Ine ndidzampatsa iye Moyo wosatha, ndipo ndidzamuwukitsa iye mmasiku otsiriza.” Ife timawopa chiyani?

140 Tamvetsera kwa ine, m'bale wanga wotopa. Baibulo linanena kuti, “Yesu anali Mwanawankhosa wa Mulungu wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.” Zindikirani. Oh, mai! Momwe izi zimawotchera mtima wanu! Momwe izi zimakupatsirani inu chiyembekezo! Mmbuyo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, pamene Satana anapotoza, woyipayo; Mulungu, pokhala wopandamalire, anayang'ana pansu kudutsa mtsinje wa nthawi, ndipo anawona mapeto.

141 Kudziwiratu! Ngati Iye samadziwa zinthu zonse, inu mwamuyikira malire Mulungu, mwamupanga Iye kukhala ndi malire monga inu ndi ine. Koma, Mulungu ndi wopandamalire; mphamvu ya Mulungu, chidziwitso cha Mulungu, chirichonse. Iye ndi Wamphamvuzonse.

142 Mmbuyo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, pamene Satana anachita choyipacho, chifukwa Satana anali nacho mmalingaliro ake chimene iye akanati adzachite, ndipo

Mulungu anawona momwe Iye akanakhoza kutsutsira icho. Amen.

<sup>143</sup> Baibulo linati, “Pachiyambi panali Mawu,” Yohane Woyera 1, “ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu,” pachiyambi, pamene nthawi inayamba. Iwo unali Muyaya, izo zisanachitike, izi ziri mu nthawi, imene ife tikuikamba.

<sup>144</sup> Muyaya uli ngati a—mawonedwe. Iwo siuma—iwo siumatha. Ndi mkombero, chopitirira kosatha ndi kosatha ndi kosatha. Ndi gudumu losatha limene siliyima kapena liribe mapeto. Koma Satana anayika choyimikira mmenemo, ndipo anadzabwera pansu apa ndipo akanadzawononga chinthu chonsecho.

<sup>145</sup> Koma, Mulungu anawona pamene pakanati padzakhale danga la nthawi. Ndipo pokhala Mmodzi wamkulu wopandalalire, kuchokera ku chiyambi mpaka ku chiyambi, Iye anayang’ana pansu. Ndipo Iye anali, pachiyambi, Mawu. Tsopano, mawu ndi lingaliro lofotokozedwa. Mulungu anayamba kuganiza, pamene Iye ankayamba kumuwona munthu aliyense amene anabwerapo pa dziko lapansi, ndi mbalame iliyonse, ndi utitiri uliwonse, ndi ntchentche iliyonse. Aleluya! Ameneyo ndi Mulungu wopandalalire, Wamphamvuzonse, Wamuyaya, wopezeka konsekonse. Ameneyo ndi Amene ife tikumutumikira mmawa uno.

<sup>146</sup> Kumbuyo komwe pachiyambi, ndipo Iye anawona kuti panali anthu ena amene akanati akhumba kuti apulumutsidwe, anthu ena amene akanafuna kupulumutsidwa, anthu ena amene ati adzakhale okhulupirika mu mtima mwawo. Iwo ankafuna kuti adzapulumutsidwe. Kenako, Iye akuyenera kupanga kukonzekera kwa chipulumutso chawo, uko nkulondola, kapena iwo sadzapulumutsidwa konse. Ndipo Iye amadziwa kuti chirichonse chopanda ungiro sichingalowe Kumwamba, chotero Iye akuyenera kuwapangira iwo njira ya ungiro. Amen. Inu mukuziwona izo?

<sup>147</sup> Ndiye, kumbuyo uko, Iye anati, “Ine, Inemwini, ndidzatsikira ku dziko lapansi ndipo ndidzakavala thupi la munthu, ndipo ndidzalipira chilango chimene chikufunika apa. Ndipo Ine ndidzatenga malowo, ndipo Ine ndidzawapanga iwo angwiro chifukwa Ine ndidzawabweretsa iwo mwa Ine, ndipo Ine ndi wangwiro.”

<sup>148</sup> Kenako pamene Yesu anati, “Chifukwa chake khalani inu angwiro, monga iwo amene ali . . . Mulungu ndi wangwiro.”

<sup>149</sup> Kenako apa panali thupi lophwanyidwa ili lomwe linamenyedwa ndi kutunduzidwa chifukwa cha tchimo, ndipo tchimo lililonse limene dziko linayamba lakhalapo nalo kapena likanati lidzakhale nalo, linayikidwa pa Iye. Ndipo Iye ali thupi limene Yehova analiwukitsa pa tsiku lomaliza kumeneko, pa tsiku lachitatu pambuyo pa imfa Yake.



<sup>150</sup> Ndipo ngati ife tiri mu Thupi limenero, ndife angwirowo basi monga Thupi liriri. Amen. Ndi zimenezotu. Mumalowa bwanji mu Thupi limenero? Inu mumalowamo bwanji mwa Ilo? Baibulo linanena, mu Aroma 8:1, “Chotero palibe kutsutsidwa tsopano kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene samayenda motsatira thupi, koma Mzimu.” Iwo samasamala zomwe dziko limanena, kapena zomwe wina aliyense amanena, kapena zomwe banja lawo limanena. Iwo amayenda mu Mzimu wa Mulungu, mu chikondi changwirowo, Chaumulungu. Inu mukuona zimenezo?

<sup>151</sup> Inu mumalowamo bwanji mwa Iwo? Pojowina mpingo? Pogwirana chanza? Ndi ubatizo wa m’madzi? Ayi, bwana.

<sup>152</sup> Mutu wa 12 wa Akorinto Woyamba unati, “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo timadzakhala ziwalo za Thupi limenero.” Ndipo, ndiye, si zimene ine ndachita, zomwe ine ndiri, chimene ine ndinali, kapena palibe kanthu za izo. Ndi chimene Mulungu wandichitira ine, mwa Khristu, ndipo ife timapangitsidwa angwirowo ndi Nsembe yathu.

<sup>153</sup> Iye samalakwitsa ayi. Iye sakanakubweretsani inu mkati ngati mukanakhala kuti sindinu oyenera. Iye amadziwa mtima wanu. Izo nzoona. Iye amadziwa chimene inu muli. Iye amadziwa zolinga zanu. Iye amadziwa chimene inu muli. Pali misampha pa njira yonse. Ndithudi, mdierekezi adzakupangitsani inu kuti muzipunthwa. Ndipo inu muziti, “Ine sindimatanzauza kuti ndichite zimenezo. Mulungu, Inu mukudziwa izo.” Inu mukadali wangwirowo chifukwa pamakhala Magazi angwirowo operekedwera inu, tsiku lililonse, ndi Nsembe yowukha magazi yapachikidwa pamaso pa Mpandowachifumu wa Mulungu Wamphamvuzonse. Izo nzoona. Tsopano, inu munalowa bwanji Mmenemo? Mulungu, mwa kudziwidwiratu. . .

<sup>154</sup> Tsopano, Mulungu ananena kuti Yesu. . . Tsopano valani zipewa zanu. Tsegulani mtima wanu. Penyani. Baibulo linati, “Yesu anali Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku” (kuti?) “maziko a dziko lapansi.” Iye anaphedwa. Chifukwa chiyani? Mulungu, Atate, pamene Iye anayang’ana pansu ndi kuwona momwe. . .

<sup>155</sup> Yesu sanangobwera kuti adzangofa imfa yachisawawa. Iye sanabwere, kudzangoti, “Chabwino, mwinamwake wina adzamva chisoni akadzawona momwe Ine ndinafera, chirichonse.” Ayi. Ayi. Mulungu samachita ntchito Yake monga choncho. Mulungu amachita ntchito Yake mwangwirowo. Uko nkulondola.

<sup>156</sup> Iye ankadziwa ndendende chimene chikanati chidzachitike. Umo ndi momwe Iye ankakhoza kuneneratu. Iye amadziwa ndendende chimene Iye. . . “Iye safuna kuti aliyense adzawonongeke.” “Iye sakufuna,” koma, ngati Iye ali wopandamalire, Iye akudziwa amene adzatero ndi amene

sadzatero. Chifukwa chake, inu mutha kukhala otsimikizika, ngati mwamulandira Mulungu ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, inu mwazikika mpaka kopita kwanu Kwamuyaya. Molondola. Mwaona, Iye amadziwiratu.

<sup>157</sup> Tsopano penyani. Baibulo linanena, kuti, “Yesu, Mwanawankhosa, anaphedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe nkomwe.” Oh! Ine—ine ndikudziwa kuti ndimachita moseketsa kuno, koma ine—ine—ine ndikumverera mwaulemlero. Taonani. Chiyani? Yesu anaphedwa dziko lapansi lisanakhale nako konse kachidutswa ka dothi. Yesu anali ataphedwa kale. Bwanji? Chifukwa Mulungu. . . Ndi ichi apa. Mumvetse izo. Mulungu, mwa kudziwiratu, pamene Iye anali Mawu pachiyambi, Iye anazindikira lingaliro. Tsopano ilo ndi lingaliro chabe; ndiye pamene Iye anayankhula, ndipo anati chidzachitika, Yesu anaphedwa miniti yomweyo imene Mulungu anayankhula Mawu. Ndiye chiyani? Patadutsa zaka foro sauzande, Iye anabwera ndipo anadzalipira mtengowo, umene Mulungu anali atachita kale kumbuyo kuno, mwa Mawu Ake. Iye ankayenera kuti abwere. Adierekezi onse ku gehena sakanatha kumuletsa Iye kubwera. Mulungu anali atayankhula kale izo.

<sup>158</sup> Tsopano, wokhulupirira, kodi mwavala nsapato zanu zachisangalalo? Mvetserani ku ichi. Ngati inu muli Mkhristu, ngati inu mulidi mwana wa Mulungu, Baibulo linati. . .

Izo si, “Oh, mlaliki!”

<sup>159</sup> Limenero ndi Baibulo. Ilo linati, “Maina anu analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Oh, mai! Nthawi yomweyo imene Khristu. . . imene Mulungu anati Khristu adzaphedwa, Iye analemba dzina lanu ndi Lake. Aleluya! Ndi zimenezotu. Dzina lanu linalembedwa. . .

<sup>160</sup> Iye anati, “Ndipo iye anawanyenga onse, aakulu, aang’ono,” ambiri anali mamembala a mpingo, Akhristu onyengezera. “Iye anawanyenga onse amene maina awo sanalembedwe,” osati mu bukhu la mpingo, koma, “mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa” (liti?) “maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.” Mulungu analemba dzina lanu mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, mwa Mawu Ake oyankhulidwa. Ndipo anamutumiza Khristu, Nsembe, kuti akagule ilo, kuti akawombole gulu lomwelo limene Iye analemba maina awo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

<sup>161</sup> Tsopano, “Iwo amene Iye anawaitana, Iye wawalungamitsa.” Iye anawaitana iwo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. “Iwo amene Iye anawayitana, Iye wawalungamitsa. Ndipo iwo amene Iye wawalungamitsa, Iye wawapatsa kale ulemelero.” Mulungu yemweyo, amene maziko a dziko lapansi

asanakhazikitsidwe, anatchula dzina lanu ndipo analilemba ilo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa; mu Bukhu, kuchokera ku maziko a dziko lapansi, anakupangirani kale malo mu Ulemelero. “Ndipo pamene msasa wapadziko lapansi uno udzatha, tiri kale ndi wina ukutiyembekezera ife uko mu Ulemelero...?...” Ndi zimenezotu. Umenewo ndiwo Uthenga.

162 Kodi ife timadandaula ndi chiyani? Chifukwa chiyani timayenda nkumawoneka monga *chonchi*, “Chabwino, ine ndimangodabwa?”

163 Kwezani mitu yanu! Baibulo linati, “Kwezani mawondo ofooka. Ndipo mulole manja akwezedwe mmwamba, amene nthawi ina anali pansu. Mulole iye amene ali wofooka anene, ‘Ndine wamphamvu.’” Ameni.

164 Pakuti, Uthenga waperekedwa. Ndi Nkhani yabwino. Ndipo, mmawa uno, Mzimu Woyera, kupyolera mu Mawu, ukukubweretsani inu Uthenga wabwino, kuti, “Kuyambira maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, Mulungu analemba dzina lanu mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.” Adierekezi onse kuchokera ku gehena sangathe kulichotsa ilo mmenemo. Mawu a Mulungu analilankhula kale ilo. Motsimikiza basi kuti zidzachitika, monga Mulungu analilemba ilo mmenemo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe! Ameni. Atate athu Akumwamba ndi a ulemelero bwanji, mu chikondi Chake chosatha ndi chifundo Chake, kuti adzatichitira ife zimenezo!

165 Anati, “Chifukwa chake khalani inu angwiwo, monga Atate anu Akumwamba ali angwiwo.” Inu mungakhale bwanji? Pamene, si ungwiwo wanga, si ungwiwo wanu. Ndi ungwiwo Wake, wa Mawu Ake; kuti Iye anakusankhani inu, ndipo inu simunamusankhe Iye. Ndipo Iye anakubweretsani inu mwa Khristu. Ndipo inu muli otetezedwa ndi Yesu Khristu, ndipo angwiwo basi monga Khristu anali pamaso pa Mulungu. Pakuti, inu simukuima ndi kwanu komwe. Inu mukuima mwa Iye, ndi chinthu chimodzi, “Ine ndikumukhulupirira Mulungu.” Ameni. Oh, ine ndimamukonda Iye! Oh, mai!

166 Kumbali ina ya Edeni, ameni, ndi nthawi yopambana bwanji imene iti idzakhale tsiku lina, pamene inu mudzayang’ana mmbuyo pansu ndi kudzati, “Nchifukwa chiyani ine ndinkawopa? Taonani chisangalalo chimene ine ndinachiphonya.”

167 Mnyamata, mtsikana, mmawa uno, kapena inu bambo wachikulire kapena mkazi, amene simunakhalepo Mkhristu, Mulungu wakhala akugogoda mosalekeza mu mtima mwanu. [M’bale Branham anagogoda pa guwa—Mkonzi]. Oh, inde, mukhoza kubwera kumapeto kwa msewu, koma simudzakhala ndi chisangalalo. Sipadzakhala nyenyezi zokuzungulirani inu kuti ziwale. Ine sindikufuna kudzayima monga choncho.

168 Ndikufuna ndidzamumve Iye akuti, “Izo zinachitidwa bwino, mtumiki Wanga wabwino ndi wokhulupirika.” Ine ndikufuna ndidzamuwonetse Iye kuyamikira kwanga.

169 Mkazi wanga wosauka, wamng’ono, wokalamba wa mutu wa imvi, momwe ine ndingakondere kumuchitira iye chinachake, chimene ndikudziwa kuti iye amachikonda, chifukwa ndimamukonda iye, ndipo ndimadziwa kuti iye amandikonda ine. Ndipo ngati ine ndingachitire izo kwa mkazi wanga, mu chikondi chaumunthu, kodi ine ndikuyenera kuchita chiyani, kuti ndidziwe kuti Mulungu, mwa chisomo, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, anandiwona ine; wosauka, wochimwa wamng’ono ndikudzandima, ndipo ndimapita ku gehena ndipo sakanachitira mwina? Ndipo Iye anandidzozeratu ine, ndipo anayika dzina langa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Oh, ine ndimamukonda Iye! Palibepo njira nkomwe, yofotokozera konse...?...Nzosadabwitsa Baibulo linanena, “Diso silinawone, khutu silinamve, ngakhalenso izo sizinalowe mmitima ya anthu.” Oh, mai! Mulungu ndi waulemelo bwanji! Kodi inu simukufuna kumudalira Iye, ngati mwatopa ndi kugwedezeke?

170 Manyazi pa inu Akhristu, amene mumadzitcha nokha Akhristu, ndipo mumayendayenda ndi kutopa. “Chabwino, ine sindikudziwa. Ndipo ngati ndipita ku tchalitchi, a...” Oh, ndinu chowiringula choyipa.

171 Ndiloleni ine ndikuuzeni inu. Kwezani mitu yanu. Wongolani chidali chanu. Oh, mai! Oh, gwiritsani ntchito chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndi bwana. Uko nkulondola. Chikhulupiriro chiri ndi tsitsi pachidali chake. M’bale, ine ndikutanthauza, chiri ndi akatumba aakulu. Pamene icho chiyankhula, nkhaba zonse zimagwa kuchokera mbali imodzi kupita ku inayo.

172 Mdierekezi amati, “Tsopano, iwe sungakwanitse basi kuchita zimenezo. Iwe sungathe kuchita izi. Iwe umachita manyazi kuchitira umboni.”

173 Chikhulupiriro chimadzukapo, nkuti, “Khala chete! Ndatenga malo.” Ameni. Ndithudi. Chikhulupiriro chimayamba kuchitapo kanthu. Ndicho chimene ife tikuchisowa lero kwa mwendamnjira aliynense mdzikoli. Wongolani mutu wanu.

174 Baibulo linati, “Pamene ine ndinali...” Davide anati, “Pamene ndinali ndi mantha, ndinkayenda ndi... Ndinkamudalira Iye. Pamene ine ndinkachita mantha, ndiye ine ndinkamudalira Iye. Nthawizonse ndikafika ku mantha a imfa, mithunzi...”

175 Pamene Paulo anatsika, iye anati, “Imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti?” M’bale...

Miyoyo ya amuna aakulu onse imatikumbutsa ife

Tikhoza kupanga miyoyo yathu kukhala  
yapamwamba,  
Ndi kusiyana, kumasiya mmbuyo mwathu  
Mphondero pa mchenga wa nthawi.

<sup>176</sup> Tsikulina, titakhala kutsidya pa mapiri akumwamba a Ulemelero, kumene dzuwa silidzalowa konse mu Mzinda umenewo, kumene oyera akufuula kale, ngwazi zakale zimenezo za Chikhulupiro, zikuyang'ana mmbuyo ku malo awo kutsidyako, ndi kumawona njira yathu, yopangidwa ndi Ulemelero. Ine ndikufuna ndidzakhale ndi iwo, ndi kudzawona kuti ine ndayika mutu wanga mmwamba mu mlengalenga ndi kumamudalira Mulungu, ndi kumayendabe mu nthawi ya namondwe. Oh, mai!

Tiyeni tipemphere.

<sup>177</sup> Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu mmawa uno chifukwa cha Yesu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha ungiro wa Uthenga, ku ungiro, ndi kuchita kwayekha Kwamuyaya kwa Mulungu Wamuyaya, Mawu oyankhulidwa. Ndipo molingana ndi Mawu Ake, Iye anatiitana ife ndipo anatisankha ife mwa Iye maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo analemba maina athu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Pamene Mulungu ayankhula mawu, izo zikuyenera kuchitika. Zikuyenera kuchitika basi. Ndipo Inu munayankhula maina athu pamene Inu munayankhula Dzina Lake. Inu munatisankha ife, ndi Iye, dziko lisanayambe, chotero palibe chimene ife tinganene kuti tikanachita, Ambuye. Izo—izo siziri mwa anthu. Palibe chomwe tingadzitukumule nacho kapena kudzitamandira. Chinthu chokhacho chimene ife tikunena, ndi, “Mulungu, zikomo Inu chifukwa cha chisomo Chanu. Zikomo Inu chifukwa cha chifundo Chanu, Ambuye. Powona kuti ife tinali alendo, koma tsopano Inu mwatipanga ife ungiro ndi Nsembe yangwiro ija imene ife taimamo, O Mulungu, tikuima mwa Iye, lero, pamene ife tikusuntha chitsogolo.” Tikukuthokozani Inu, Atate, chifukwa cha zinthu izi.

<sup>178</sup> Ife tikupempha, ngati alipo mmodzi muno lero, Ambuye, amene sali mu chikhalidwe chimenecho, mulole iwo mphindi ino apange chisankho chawo chimodzi ndi Chamuyaya ndi chomaliza, Inu musanapange kuyitana Kwanu komaliza ndi kotsiriza pa mtima wawo. Ife tikupemphera kuti Inu mupereke izo kudzera mu Dzina la Khristu.

<sup>179</sup> Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati alipo munthu woteroyo pano mmawa uno, amene alidi mwa namwali wogona; simunadzukepo ku kuzindikira kuti mukuyenera kupulumutsa miyoyo, inu mukuyenera kuchita chinachake? Ndipo mukufuna kuti Mulungu akukumbukireni, monga wopulumutsa moyo;

mukufuna kukhala mmodzi amene ati apite kunja ndi kukayesa kupulumutsa miyoyo? Kodi mungakweze dzanja lanu, kuti, “Mulungu, ndikumbukireni ine.” Mulungu akudalitseni inu. Izo nzabwino. Chabwino.

<sup>180</sup> Kodi alipo munthu woteroyo pano mmawa uno amene sanamulandirepo Khristu nthawi imodzi ngati Mpulumutsi, koma, mmawa uno, akufuna kuti apange lingaliro lotsiriza ndi Lamuyaya limenero? Pamene inu mukuona dzuwa likukalowa kutsidyako, ndipo inu mukudziwa kuti kwangotsala masiku ochepa chabe ndipo ife sitikhala kuno mopitirira. Inu mukudziwa zimenezo. Koma inu mukufuna ku—mukufuna kuti mubwere mu Ufumu wa Mulungu. Mukufuna kuti Mulungu akulandireni inu. Ndipo inu mukukhulupirira kuti Iye amachita zimenezo, ndipo inu mukweza dzanja lanu kuti muchite zimenezo, mmawa uno, kuti mukukhulupirira kuti Khristu tsopano akukutengani inu ngati mwana Wake. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu.

<sup>181</sup> Winawakenso, inu mumutenga Iye ngati Mpulumutsi wanu, lero? Inu mukweza dzanja lanu, kuti, “Kuyambira lero, kuchoka pano, tsopano ndizimutumikira Mulungu ndi mtima wanga wonse. Ine ndikukhulupirira. Ndipo ndikufuna kuti ndikumbukiridwe. Moyo wanga wonse, Chinachake chakhala chikugogoda pa mtima wanga, ndipo chagogoda pa mtima wanga, ndipo ine ndimachikana Icho. Ndipo ine ndikuwopa ine ndikhoza kuchikana Icho nthawi yolakwika tsopano. Ndipo chotero, mmawa uno, Mulungu, mwa chisomo, ine ndikutulukira ndi kukweza dzanja langa, ndikuti, ‘Ndichitireni chifundo ine, wochimwa’?”

<sup>182</sup> Kodi pangakhale wina? Mulungu akudalitseni inu. Ndipo akudalitse iwe, mtsikana wamng’ono. Ndawona dzanja lako, nawenso, wokonedwa. Chabwino. Winawakenso, kodi mungakweze dzanja lanu, mukuti, “Ndikumbukireni ine?”

<sup>183</sup> Kodi alipo wobwerera mmbuyo, ndipo akuti, “Oh, M’bale Branham, ndine Mkhristu, koma ndine wowiringula wosauka pa mmodzi. Kawirikawiri ndimabwerera mmbuyo ndipo ndimachita zolakwika. Ndipo ine—ndimamukonda Mulungu. Mulungu ananditenga ine mwa chisomo. Ndikudziwa kuti ndine mwana Wake. Koma sindinakhalepo wokangalika, sindinachitepo ntchito ya Ambuye. Ine mwanjira ina ndimangotengeka motsatira, ndi kulowa ndi kutuluka, ndi kulowa ndi kutuluka. Koma Chinachake chimangondigwira ine, mu mtima mwanga. Ndikuchita manyazi ndi umboni wanga. Ine ndingachite manyazi kukomana ndi Mulungu, mmawa uno, osati moyo umodzi kapena kalikonse. Ine—ine—ine ndikufuna Mulungu andibweze ine ndi kundikumbatira ine ku mbali Yake yowukha magazi, ndi kundikwapula ine, chimene ine ndikuyenera, ndi kundilola ine ndikhale Mkhristu weniweni kuyambira lero, mpakana. Ndikwezera dzanja langa

kwa Mulungu. Ndi chimene ine ndikufuna kuti Inu muchite, Mulungu.”

<sup>184</sup> Mulungu akudalitse iwe, dona. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Kutu, tsopano Mulungu akuwona mtima wanu. Ndipo ambiri a inu munakweza manja anu, ine ndikukudziwani inu. Ine ndimadziwa moyo wanu wokwera-ndi-wotsika. Pamene inu. . . (Akhristu ena onse akupemphera.) Ine ndikudziwa chikhalidwe chanu chokwera-ndi-chotsika. Ine ndikudziwa kubwerera mmbuyo kwanu. Mulungu amazidziwa izo mwabwino kwambiri, ngati ine ndazidziwa izo. Ine ndikukuwonani inu mukubwera ku guwa, kuyesera kuti mudzapange poyambira, ndi kubwerera mmbuyo; kuyesera kuti mupange poyambira, ndi kubwerera mmbuyo.

<sup>185</sup> Mwamuna anangogwa nkufa, masiku angapo apitawo, amene ankaphunzitsa Sande sukulu kuno. Ine ndikuwopa ena a anthu ake ali pano. Ine ndikanatchula dzina, ambiri a inu mukudziwa amene ine ndikumukamba. Munthu ameneyo ankabwera ku tchalitchi, iye ankabwerera; iye ankabwera ku tchalitchi, iye ankabwerera. Iye ankafuna kuchita bwino. Iye anali ndi chomuchitikira ndi Mulungu. Iye anali munthu wabwino, mu mtima, koma iye anayamba kusokonezeka kwambiri ndi dziko. Iye anafa, ali mnyamata. Analisiya dziko lapansi. Tsopano ndikudabwa kuti mphotho yake idzakhala chiyani. Mukuona? Musachite zimenezo. Musamachite zimenezo, mzanga. Mukhale mzingwezo.

<sup>186</sup> Munthu ameneyo atakhoza kubwerera ku dziko lapansi lero, ndi kudzayima kutsidya mu mzinda, paliponsepo, pamalo omwewo amene iye anaferapo, iye angadzafuule ndi kuthamangira ku kachisi molimba momwe iye akanatha kubwerera. Mnyamata, ine ndikukuuzani inu, pangadzakhale miyoyo yopulumutsidwa sabata yamawayi, iye atati wadzafika kuno. Iye ali kutsidya kwa mzere tsopano. Koma, kumbukirani, bola ngati Muyaya ulipo, mwakuya monga mlengalenga ulipo, iwo sadzakhala ndi mwayi wina woti apulumutse moyo, sadzakhalanso ndi mwayi wina wodzakhallira moyo Mulungu. Iye anapanga chisankho chake chomaliza.

<sup>187</sup> Nanga bwanji zanu, mmawa uno? Tiyeni tizikonze izo, kwa Mulungu, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Tipatseni ife poyambira pang’ono, “Kutsidya lina la Yordano.”

Ku ina . . .

Tsopano pitirizani kupemphera.

. . . wa Yordani,  
Mmindanda yokoma ya Edeni,

Pang’onopang’ono tsopano, tonsefe.

Kumene Mtengo wa Moyo ukuphukira,  
Kuli mpumulo wanu.

Yesu amaswa unyolo uliwonse,  
 Yesu amaswa unyolo uliwonse,  
 Yesu . . .

Chikukulepheretsani inu ndi chiyani?

. . . unyolo uliwonse,  
 Pamene Iye amakumasulani!

Ine nthawizonse, ndidzamtamanda Iye,  
 Ine nthawizonse, ndidzamtamanda Iye,  
 Ine nthawizonse, ndidzamtamanda Iye,  
 Pakuti Iye amandimasula ine!

Tsopano tonsefe, pamodzi, pang'onopang'ono.

Kutsidya lina la Yordano, (Kutsidya la mtsinje  
 uko.)

Mminda yokoma ya Edeni  
 Kumene Mtengo wa Moyo ukuphuka,  
 Kuli mpumulo wanu.

Bwanji, Yesu amaswa uliwonse . . .

<sup>188</sup> Maunyolo osayanjanitsika, maunyolo achipembedzo,  
 maunyolo achipembedzo, unyolo wautchimo, unyolo wa  
 kusakhulupirira.

Yesu . . . (Kukhalapo Kwake kuli pafupi) . . .  
 unyolo uliwonse,

Mungopanga chisankho chanu.

Pamene Iye anakumasulani inu!

Ine nthawizonse, ndidzamtamanda Iye,

Mulungu akudalitseni inu, dona.

. . . pembedza Iye,

<sup>189</sup> Winanso, mulole maunyolowo aduke mozungulira. Kodi inu  
 simukufuna kukhala mfulu, lero? Mukungonamizira chiyani?  
 Bwanji, ndinu womvetsa chisoni kwa inueni, ngati simuli  
 mfulu; Mzimu Woyera, zidutswa zonse zichoke panjira, Mzimu  
 wa Mulungu ukusunthira pansu mu mtima mwanu. Mulungu  
 akudalitseni inu, mlongo.

Kumbali inayo . . .

<sup>190</sup> Mwinamwake chinthu chaching'ono chakale  
 chikukugwirani inu. Kodi inu simukufuna kupulumutsidwa?  
 Ndikudalira kuti maina athu akulungidwa pamodzi. Mulungu  
 akudalitseni inu, m'bale. Ine ndikuyembekeza maina athu  
 akulungidwa pamodzi, uko mu Ulemelero, monga nyenyezi za  
 Mulungu, zikuwala kwanthawizonse. Mudzayang'ane kumeneko  
 ndipo mudzati, "Ndi uyo wayimayo M'bale Branham."

<sup>191</sup> Ine ndidzati, "Oh, eya, m'bale. Mukukumbukira kumusi ku  
 kachisi mmawa uja?"

. . . ukuphuka,



Kuli mpumulo wanu.

Ine nthawizonse, ndidzamtamanda Iye  
nthawizonse, (Kodi inu simukufuna kuchita  
zimenezo?)

. . . nthawizonse, ndidzamtamanda Iye  
nthawizonse,  
Ine . . .

192 Wobwerera mmbuyo, kodi iwe sukufuna kusunthira ku guwa  
tsopano?

. . . nthawizonse . . .

Chinachake chachikale chaching'onocho chayima mnjira  
yako. Yesu amaswa unyolo umenewo. Kazibwerani.

Pamene Iye amakumasulani inu!

Pamtanda pomwe Mpulumutsi anafera,

Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;

Oh, pamenepo pa mtima wanga Magazi  
anapakidwa;

Ulemelero ku Dzina Lake!

Oh, ulemelero kwa Dzina Lake lofunika!

Oh, ulemelero . . .

193 Mzanga wochimwa, pano pa guwa, wobwerera mmbuyo,  
muwuzeni Iye za izo tsopano. Izo zinali kuti?

Pamenepo kumtima wanga panali . . .

194 Inu mwagwada pamenepo nokha ndi Mulungu tsopano. Iye  
akuyang'ana pa inu. Palibe ngakhale mpheta ingagwe popanda  
Iye kudziwa izo.

Oh, bwerani ku Kasupe wolemera kwambiri,  
wokoma, wofewa,

195 Ngati inu simunalandirepo Mzimu Woyera, bwerani. Iye ali  
pano.

. . . pa mapazi a Mpulumutsi;

Oh, gweranimo lero, ndipo mupangidwe  
kukhala amphumphu;

Oh, ulemelero kwa Lake . . . (Gwirani  
pamenepo tsopano.)

196 Pamene mitu yanu ili yoweramitsidwa. Kodi inu munayamba  
mwawazindikirapo anthu amene amalandira Khristu?  
Penyani mtundu wa malo amene iwo analipo, momwe  
iwo anawupezera Iwo, inu mudzawawona iwo akuchita  
mofanana. Ndithudi. Ngati ziri zampatuko, ndi zongokonza  
ndi zotengeka, mwanayo adzawukitsidwa monga chomwecho.  
Umo ndi momwe zidzakhali. Ngati ziri zozizira, zofunda,  
komanso zosayanjanitsika; kawirikawiri momwe iwo aliri. Iwo  
amalandira mzimu wa mtundu umenewo, chifukwa ndi chimene  
chiri pamenepo chikugwira ntchito pamenepo.

<sup>197</sup> Nditengereni ine ku mtanda. Nditengereni ine ku malo kumene kuli Mzimu ukuyenda, izo zimafewetsa mtima wanga. “Ngakhale ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi a Angelo, ngakhale ndingapereke chuma changa chonse kuti ndidyetse osauka, thupi langa kuti liwotchedwe ngati nsembe, kukhala ndi chidziwitso kudziwa zinsinsi zonse ndi zinthu zonsezi, izo zonse zidzalephera. Koma pamene icho chimene chiri changwiwo chidzabwera, chimene chiri chikondi, icho chimapirira kwanthawizonse.” Chikondi chimachita chikhulupiriro.

<sup>198</sup> Kodi inu simubwera tsopano pamene kumverera kokondeka uku, kodzichepetsa, kokoma kwa Mzimu Woyera kukusunthira apa pa guwa tsopano. Mungogwada pansi, nenani, “Mulungu, mundichitire ine chifundo. Ine ndikufuna Inu mundipatse ine tsopano, mu mtima mwanga, Mzimu uwu umene uli mu mpingo. Tsopano ndikugwada, ndipo ndikupempha. Ndipo, mwa chikhulupiriro, ine ndikukhulupirira kuti Inu mupereka izo kwa ine.” Muziyenda mukuchoka pano, umodzi wa mizimu yodzichepetsa kwambiri, yokoma kwambiri. Zonse zidzakhala zitatha pameneipo.

Ndapulumutsidwa modabwitsa ku tchimo,  
Yesu amakhala mkati mokoma,  
Oh, pa mtanda pamene Iye ananditengera ine  
mkati;  
Ulemelero ku Dzina Lake!  
Ulemelero . . .

<sup>199</sup> Pamene ife tikuyimba iyi, ndikudabwa ngati pali Akhristu omwe angafune kudzipatula moyo wawo ndi awa pano pa guwa, amene abwerera Mzimu Woyera ndi chipulumutso. Kodi inu mungafune kugwada pano ndi ife, kupemphera ndi ife kwa maminiti pang’ono? Chirichonse chimene inu mukuchifuna, ziribe kanthu chimene icho chiri. Ngati ali matenda, inu mukufuna machiritso. Ngati liri vuto, ndipo mukusowa mpumulo, ngati muli ndi nkhwana kuvutitsidwa, mukufuna—mukufuna mtendere, bwerani tsopano, simutero inu?

Oh, bwerani ku Kasupe uyu wolemera ndi  
wokoma;  
Perekani moyo wanu wosauka pa  
Mpulumutsi . . .

Wokondwa kwambiri kuwona ambiri akubwera, mmawa uno.

. . . lero ndi kukhala amphumphu;  
Ulemelero kwa . . .

<sup>200</sup> Inu mwaona, ndi ntchito ya Mzimu Woyera. Iye amachita izi. “Ku . . .” Osati motengeka. Zolimba, zakuya. Osati

motengeka. Sizovomerezeka. Ndi chikondi chimene chimakoka, chimatikakamiza ife.

Pamenepo ku mtima wanga Magazi  
anapakidwa;  
Oh, ulemelero ku Dzina Lake!

<sup>201</sup> Zopambana! Aliyense akungowerama tsopano. Kodi simukuzikonda izi? Sindikudziwa momwe inu mukumverera, koma ine ndikungomverera ngati, mu mtima mwanga, iwe umangomverera kugwa kwa misozi mkati mwako, ikutsikira pansi. Mzimu Woyera wa Mulungu ukungoyenda, Iye akuichita ntchitoyo. M'bale, ndipatseni ine mpingo wonga umenewo, umene uli wosweka kwenikweni, ukupita ku nyumba ya Wowumba, kuti ukawumbidwenso.

Yesu, mundisunge pafupi ndi mtanda,  
Pali Kasupe wantengo wapatali,  
Waulere kwa onse. . .

<sup>202</sup> Tiyeni omvetsera athandizire kuiyimba iyo tsopano, pamene olapa ali pa guwa, akupempha.

Umayenda kuchokera ku Kasupe wa Kalvare.  
Mu mtanda, mu mtanda,  
Oh, ukhale ulemelero wanga nthawizonse;  
Ndipo moyo wanga wokwatulidwa udzapeza  
Mpumulo kutsidya kwa mtsinje.

<sup>203</sup> O Mulungu, Atate athu, ife tikubwera kwa Inu, lero, modzichepetsa, osweka. Mzimu Woyera ukubwera mu Mawu. Akhristu ndi kwambiri oya- . . . ndi oyamikira kwambiri kwa Inu, kuti akulandirani Inu, abadwa mwatsopano. Inu munadzoza izi kuyambira ku maziko a dziko lapansi. Inu munalengeza izo. Inu munati, "Ndiri ndi zinthu zambiri zoti ndikuuzeni inu, zimene sindingathe kukuuzani inu tsopano. Koma pamene Iye Mzimu Woyera adzabwera, Iye adzaulula zinthu izi kwa inu, ndipo adzakuphunzitsani inu ndi kukutsogolerani inu." Ndife othokoza kwambiri, mmawa uno, chifukwa cha Mzimu Woyera umene umawulula Mawu a Mulungu. Inu munati, "Ndipo Iye adzabweretsa zinthu izi kwa Anga . . . kwa chikumbutso chanu, zimene Ine ndanena kwa inu. Ndipo Iye adzakuwonetsani inu zinthu zimene ziri nkudza."

<sup>204</sup> Ndife okondwa kuti Iye ali ndi ife lero. Ndipo kudzera mu kuphunzitsa kwa Mawu, ndi kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera, kwapangitsa Akhristu kudzuka, zinapangitsa ochimwa kuti abwere kwa Inu, obwerera mmbuyo kuti adzadziyeretsenso okha. Atate, iwo ali pa guwa. Zipangitsa odwala ndi otopa, omwe asautsidwa, kuti abwere ndi kudzaweramitsa mitu yawo, kuti adzavomereze machiritso a thupi lawo, podziwa kuti Mawu Anu oyankhulidwa ndi Choonadi. China chirichonse chidzalephera, koma Mawu Anu sangalephere konse. Choonadi! "Inu mudzadziwa Choonadi, ndipo Choonadi chidzakumasulani."

205 Ndipo ife tikubwera kudzavomereza, mmawa uno, chimene Inu mwatipatsa ife, mu kuzunzika Kwanu kopambana ndi chitetezero, pa imfa Yanu, imene Inu munatipangira ife. Ndipo ife mwaulere, Ambuye Yesu, tikulandira izo. Ife tikukhulupirira Mawu a Mulungu. Tikukhulupirira kuti Inu munalonjeza, “Iye amene adzadza kwa Ine, Ine sindidzambutaya konse.” O Mulungu, ndi lonjezo lotani! Ziribe kanthu kuti ndi zachiyani, Inu mwatero, “Pamene mupemphera, khulupirirani kuti mwalandira chimene mwapempha. Inu mudzalandira icho.”

206 Tsopano, Atate, ngati ife tikukhulupirira izo mooni, izo zakhazikika. Ife tikukhulupirira izo. Izo zachitika. Ndiye ife tikuchita pa kuvomereza kwathu, kuti Inu mwatichitira ife izo. Osati kuti ndife oyenera; ndife osayenera. Koma kupyolera mu chisomo Chanu chosatiyenerera chimene ife tiri nacho kupyolera mwa Inu, ife tikukhulupirira kuti ntchito yatha.

207 Ndipo monga olapa awa, ndi iwo amene akubwera mmawa uno, kudzadzapatulira okha, ndi kwa iwo amene akubwera pa zopindula za zowawa, monga Davide ananena, “Lemekeza Ambuye, O moyo wanga, ndipo usaiwale zabwino Zake zonse; Amene akhululukira mphulupulu zanga zonse, ndi kubwerera mmbuyo kwanga; ndi amene achiritsa matenda athu onse.” Zimenezo ndi zopindula za okhulupirira. Ndipo ife tikuzilandira izo, kudzera mu chikhulupiriro, mmawa uno, pobwera pa Mawu a Mulungu, zimene zinayankhulidwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ngati kukanakhala kosatheka kuti izo zisachitike, momwemonso sikotheka kuti ife tisanlandire zomwe tapempha, ngati ife tapempha izo ndi chikhulupiriro tikukhulupirira. Ndipo zimenezo ziri mkati mwa mitima yathu, Ambuye, kuti tilandire zomwe ife tapempha.

208 Yesu, tisungeni pafupi ndi mtanda. Pamene mdani abwera ngati madzi ofukira, Ambuye, muzikweza mlingo motsutsana ndi iye. Dalitsani gulu laling’ono ili, loyembekezera. Mulungu, mulole Mzimu Wanu Woyera uwatenge awa amene ayeretisa miyoyo yawo, amuna ndi akazi awa amene anagwada pa guwa. Ochimwa awo amene anabwera ndi kudzaweremitsa mitu yawo, atengereni iwo mu Ufumu Wanu.

209 Ambuye, ndikuzindikira kuti ndi chikhulupirira chawo chomwe, miniti imene iwo anakukhulupirirani Inu, imeneyo ndi miniti imene Inu munawalandira iwo. Pakuti Inu munati, “Palibe munthu angabwere pokhapokha Atate Anga atamukoka iye. Ndipo yense amene adza, Ine ndidzampatsa iye Moyo wosatha, ndipo ndidzamuukitsa iye pa tsiku lotsiriza.” Amenewo ndi Mawu Anu, Ambuye. Ife tikuwakhulupirira Iwo.

210 Ndipo izo zatheka, ntchitoyo yatha, ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izo. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha machiritso a thupi lirilonse, chifukwa cha

moyo uliwonse wotopa, chifukwa cha chirichonse chimene Wanu. . . Iwo amene anali ndi manja ofooka, amene akhala ali ndi mantha, iwo amene amadabwa. Davide anati, “Pamene ine ndinkaopa, ndinachita mantha, kenako ine ndinadalira mwa Inu ndipo ndinayendabe chitsogolo.”

<sup>211</sup> Mulungu, tiloleni ife tikweze mitu yathu, mmawa uno; osati amantha, koma Akhristu amene akukhulupirira mwa Yesu Khristu. Mulole ife tiziyendabe, ndi umboni wathu ukuwala. Mulole, kupyolera mu machiritso a matupi athu, kupyolera mu umboni wa chipulumutso chathu, mulole ife tipindulire ena kwa Inu. Perekani izi, Atate, monga onse pa guwa ife tazisiya. Perekani izi kwa Ulemelero Wanu, pamene ife tikukhulupirirani Inu ndi kuyembekezera pa Inu, Ambuye.

<sup>212</sup> Apa ndi pamene, kungosamba mu kukongola Kwanu, kungosamba mu lonjezo Lanu, kumverera Mzimu Woyera waulemelo uwo ukutikopera ife kwa Inu. Momwe ife timakukonderani Inu! Momwe ife tikukutamandirani Inu!

<sup>213</sup> Momwe ine ndikukupembedzerani Inu, Ambuye! Inemwini, kuno kuseri kwa desiki lopatulika ili, manja anga ali mmwamba kwa Inu, ine ndikukupembedzani Inu, Mulungu wanga. Ine ndikukupembedzani Inu. Ndinu Mchiriti wanga, Mpulumutsi wanga, Mfumu yanga, Wondipatsa wanga, Atate anga, M'bale wanga! Zonse-mu-zonse wanga akukhazikika mwa Inu. Inu ndi mphamvu zanga. Ine mwapoyera. . . Inu. . . Davide anati, “Ndidzakutamandani Inu mu msonkhano wa oyeramtima.” Ndipo ndidzakupatsani Inu matamando pamaso pa oyeretsedwa mmawa uno. Ine ndikukutamandani Inu chifukwa chondichiza ine. Ndikukutamandani Inu chifukwa cha moyo wanga. Ndikukutamandani Inu chifukwa cha thanzi langa. Ndikukutamandani Inu chifukwa cha ubwino umene Inu mwandiwonetsera ine. Ndikukutamandani Inu chifukwa cha azimzanga. Ndikukutamandani Inu chifukwa cha chirichonse, Ambuye. Ndinu wodabwitsa, chisangalalo chosaneneka komanso chodzaza ndi ulemelero! Momwe ine ndikukutamandani Inu!

<sup>214</sup> Momwe ine ndingakuvomerezereni Inu kwa ofooka! Momwe ine ndingakuvomerezereni Inu kwa wochimwa, ngati Mpulumutsi! Momwe ine ndingakuvomerezereni Inu kwa odwala, ngati Mchiriti! Momwe ine ndingakuvomerezereni Inu kwa woyendayenda, ngati Mfumu! Oh, momwe ine ndikukukonderani Inu, mmawa uno! Momwe ndingakuvomerezereni—ndingakuvomerezereni Inu, Ambuye, kwa iwo oponderezedwa, kukhala—kukhala chisangalalo chosangalatsa mumsasa! Momwe ife tikukuthokozerani Inu!

<sup>215</sup> Oh, Ndinu Thanthwe mu dziko lotopetsa, Pobisalirapo mu nthawi ya namondwe; Alfa, Omega, Chiyambi ndi Mapeto; Duwa la Sharoni, Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa!

Oh, momwe ife timakukonderani Inu! Momwe timakukonderani ndi kukulemekezani Inu, Inu wosafanizika Wamuyaya Uyo! Ife tikukupatsani Inu matamando. Oh, ife tidzakutamandani Inu, ndi kukupatsani Inu matamando, kudutsa mibadwo yonse!

<sup>216</sup> Tilandireni ife, Ambuye, pamene ife tikupereka madalitso awa, zipatso za milomo yathu. Inu munati, “Ndife anthu achilendo, ansembe achifumu, tikupereka nsembe zauzimu, zipatso za milomo yathu kupereka matamando ku Dzina Lake.” Momwe ife timamutamandira Iye! Momwe ife timamukondera Iye kwanthawizonse ndi nthawizonse! Oh, landirani zokonda za mtima wathu, onetsani milomo yathu, Ambuye, kuti kuchokera mu kuya kwa mtima woyera ife tikukutamandani Inu. Podziwa, kuti, si zomwe tingachite. Si moyo wathu; ndi Moyo Wake. Si chipulumutso chathu; ndi chipulumutso Chake. Si kumwamba kwathu; ndi Kumwamba Kwake. Oh, ife sintchito zathu zomwe; ndife ntchito Zake. Osati chisomo chathu; ndi chisomo Chake. Osati ulemelero wathu; koma ulemelero Wake. Osati mphamvu yathu; koma mphamvu Yake. Oh, momwe ife timakukonderani Inu! Osati mpingo wathu; koma Mpingo Wake. Momwe ife tikukutamandirani Inu, pakuti iyo ndi mitima yathu, Ambuye. Ndiyo mitima yathu. Tilandireni ife.

<sup>217</sup> O Mulungu, mtumizireni Branham Tabernacle wamng’ono kutsanulira kwa Mzimu. Inu mutero, Ambuye? Oh, ndife osowa, pano pa ngodya. Mulungu, tsitsani mivumbi ya mdalitso. Tsanulirani mvula ya Mulungu, yoyamba ndi yotsiriza.

<sup>218</sup> Abatizeni abusa athu, mwatsopano, Ambuye. Ayatseni iwo moto ndi Uthenga. Ife tikuwakonda iwo, lero, Ambuye. Iwo ndi wantchito Wanu. Ife tikupemphera kuti Inu muwudzoze mtima wawo.

<sup>219</sup> Mudzoze mitima ya alaliki ena mchipinda chino mmawa uno, ndi membala aliyense. Mulole ife tichoke pano, Ambuye. . .

<sup>220</sup> Ndipo musayiwale wantchito Wanu wosauka, wosayenera, inemwini, Ambuye. Kuti Inu mundidzoze ine mwatsopano ndi Mzimu Woyera. Perekani izi, Ambuye.

<sup>221</sup> Tipatseni ife madalitso awa. Ife modzichepetsa tikuyembekezera pa guwa, podziwa kuti ife tikulandira iwo, kudzisambitsa tokha mu Mzimu Wanu Woyera; ndipo osachita manyazi ndi Uthenga wa Yesu Khristu, Mphamvu ya Mulungu, ku chipulumutso. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha Izo!

<sup>222</sup> Tsiku lina laulemelero, ife tikuyembekeza kudzakuwonani Inu, Ambuye, kudzaika manja athu pa mapazi a Iye amene wayima nafe lero, amene ife sitingathe kumuona, koma ife tikudziwa kuti Iye ali pano. Momwe ife timamutamandira Iye!

. . . kumusi mu Mzinda umenewo,

Dzuwa silidzalowa konse;

Maluwa akuphukira kwa nthawizonse,

Ndipo dzuwa, silidzalowa konse.

Ndikumverera ngati ndiziyendabe, ndikutero,  
Ndikumverera ngati ndiziyendabe;  
Maluwa akuphukira kwanthawizonse,  
Ndipo dzuwa silidzalowa konse.

Ndi angati akumverera choncho? Kwezani mmwamba dzanja lanu.

. . . ndikumverera ngati ndifuule, nthawi zina  
ndimatero,  
Ndikumverera ngati ndifuule, ndikutero;  
Maluwa akuphukira kwanthawizonse,  
Ndipo dzuwa, silidzalowa konse.  
Ndikumverera ngati ndiziyendabe, ndikutero,  
Ndikumverera ngati ndiziyendabe;  
Maluwa akuphukira . . . ( . . . ? . . . )

<sup>223</sup> Inu ndi Mmodzi muli pamutu pa ngalawayo, Ambuye. Inu mukudziwa zonse za izo. Ife tikupempha mdalitso uwu mu Dzina la Khristu. Amen.

<sup>224</sup> Wokonedwa Atate Akumwamba, pamene tikudutsa pa guwa, kuyika manja pa iwo amene mwina akuyembekezera mdalitso wowonjezera, mulole Mzimu Woyera, umene sunakhudze basi mwanjira yoyenera . . . Koma ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mupereke mdalitso . . . ? . . . Oh, yankhulani, Atate Akumwamba, chitirani chifundo mlongo wathu.

<sup>225</sup> Wokonedwa Atate Akumwamba, pamene mkazi wokonedwa uyu apa akubwera kuno mwa chikhulupiriro . . . Masiku ambiri iye wakhala ali kuno; imvi izi ndi makwinya awa . . . ? . . . Koma ndi khama lochuluka bwanji limayenera kuti adutse pano. Mosakaika koma chimene manja awa abwera pansu pa masamba a Baibulo, atakwezedwa mmwamba kwa Inu. Mosakaikira, koma wona mu mtima, mmawa uno, pamene iye amatsimphina akulowa mu tchalitchi chino, ali ndi ndodo pansu pa nkono wake. Koma tsopano, mwa chikhulupiriro, iye waziyika izo pansu, kuti achoke akuyenda. Mchiritseni iye, Ambuye. Iye wabwerera madalitso a Mulungu. Ine ndikupemphera, Mulungu wa Kumwamba, kuti Inu mumudalitse iye. Ndipo mulole iye asadzaisowe konse iyo, masiku ake onse. Mpateni iye mphamvu mu thupi lake. Mulole iye akapindulire miyoyo kwa Inu, Ambuye, ku Ufumu wa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

<sup>226</sup> Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Musati . . . Simukasowanso kukagwiritsa ntchito ndodo yakaleyo, ine sindikukhulupirira, aponso. Inu muli bwino bwino, ndipo ine ndikukhulupirira kuti mukupita kwanu wopanda iyo. Amen. Pamene muzituluka mchipindachi, muiyike iyo paphewa panu, ndi kumatuluka. Zonse zikhala zitatha.

<sup>227</sup> Atate Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse mkazi uyu amene wayima pano lero. Mumupange iye akhale wamphumphu. Perekani izi, Atate. Ife tikuyika manja pa iye ndi kukhulupirira izo, mu Dzina la Yesu.

<sup>228</sup> Atate Mulungu, ife tikuyika manja pa Mlongo Slaughter, ndikupempha kuti iye achiritsidwe. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

<sup>229</sup> Wokonedwa Mulungu, ife tikuyika manja pa athu. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

<sup>230</sup> Sindikudziwa momwe mukumverera. Ndiyimba vesiyo; inu muyimbe kolasi ndi ine.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera ili,  
Anali Yohane M'batizi, iye anafa ngati munthu;  
Kenako anabwera Ambuye Yesu, iwo anamupachika Iye,  
Iye analalikira kuti Mzimu udzapulumutsa anthu ku tchimo.

Ukuwukhabe magari, inde, ukuwukha magari, Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, (Ine ndikuukonda Iwo.) ukuwukha magari, Magazi a ophunzira (Lisiyeni dziko linene chimene iwo akufuna.) amene anafera Choonadi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukhabe magari.

Kenako anamugenda Stefano, iye analalikira motsutsa tchimo  
Iye anawakwiyitsa iwo, iwo anaphwanyira mutu wake mkati;  
Koma iye anafa mu Mzimu, napereka mzimu, Ndipo anapita kukalumikizana ndi ena, khamu lopereka moyo.

Anapitirira kuwukha magari. . .  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha magari,  
Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha magari.

Kunali Petro ndi Paulo, ndi Yohane waumulungu,  
Iwo anapereka miyoyo yawo kuti Uthenga uwu uwale;  
Iwo anasakaniza magari awo, ndi aneneri akale,



Kuti Mawu owona a Mulungu akhoze  
kunenedwa moona.

Ukuwukhabe magazi, inde, ukuwukha magazi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha  
magazi,

Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha  
magazi.

Miyoyo pansi pa guwa, ikulira, “Mpaka liti?”  
Kuti Ambuye alange amene anachita zoyipa;  
(Mvetserani.)

Koma padzakhala ochuluka omwe adzapereke  
magazi a moyo wawo,  
Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu  
ndi kusefukira kofiira.

Oh, ukuwukhabe magazi, inde, ukuwukha  
magazi,

Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha  
magazi,

Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha . . .

<sup>231</sup> Ndi angati ali okondwa mmawa uno kuti mwalandira Mzimu  
Woyera? Kwezani mmwamba manja anu. Kodi Izo sizodabwitsa?  
Ndithudi.

Ukuwukha ndi . . .

<sup>232</sup> Gwiranani chanza ndi mzanu amene wayima pafupi nanu.

. . .kuwukha magazi,

Nenani, “Ambuye alemekezeke, m’bale, chifukwa cha  
ubwino Wake wonse.”

. . .Uthenga wa Mzimu ukuwukha magazi,

Oh, magazi a ophunzira amene anafera  
Choonadi,

Uwu . . .

Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni  
inu.

. . .Uthenga ukuwukha magazi.

Oh, ukuwukha magazi . . .

Ndi zimenezotu. Kwezani mmwamba manja anu.

. . . ukuwukha magazi,

Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha  
magazi,

Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha  
magazi.

Ukuwukha magazi, (Aleluya!) ukuwukha  
magazi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, oh, Iwo  
ukuwukha magazi, (...?.?)  
...magazi, inde, Iwo ukuwukha magazi,  
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu, ukuwukha  
magazi.

Aliyense ayimbe iyo!

Magazi a ophunzira . . .

<sup>233</sup> Mulungu akudalitseni inu, mlongo. [Mlongo akuti, “M’bale Branham...?.?—Mkonzi]. Eya. [“...?.?..zaka zitatu zapitazi.”] Zopambana! Wokondwa kwambiri kumva zimenezo. [“Iye anandiuzana ine, ngati ndikanakhala ndi mwayi woyankhulana nanu, kudzakuuzani inu, ‘Moni.’”] Mulungu akudalitseni!

<sup>234</sup> Dona amene wangopemphereredwa kumene, iye wakhala akuyenda tsopano kwa zaka zitatu, akulemekeza Mulungu.

Tsopano tiyeni tiyimbe nyimbo yabwino yakale iyi. Ndi angati amayikonda iyi?

Chikhulupiro mwa Atate, chikhulupiro  
mwa Mwana,  
Chikhulupiro mwa Mzimu Woyera, atatu  
mwa Mmodzi;

Chabwino, mlongo, perekani iyo.

Chikhulupiro mwa . . . Mwana,  
Chikhulupiro mwa Mzimu Woyera, atatu  
mwa Mmodzi;  
Ziwanda zidzanthunthumira, ndipo ochimwa  
adzauka:  
Oh, chikhulupiro mwa Yehova chirichonse  
chidza . . .

<sup>235</sup> Ndi angati amakonda khamu labwino losangalala ngati ili? Bwanji, Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Tiyeni tonse tiyimbe tsopano. Aliyense, pamwamba pa mawu awo. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Zikomo inu, mlongo. Mulungu akudalitseni. Amen. Mulungu akudalitseni inu. [M’bale akuyankhula ndi M’bale Branham—Mkonzi]. Inde. Amen. Amen. Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni.

<sup>236</sup> [Mlongo akuyankhula ndi M’bale Branham—Mkonzi]. Mulungu akudalitseni inu, mlongo wanga wokondedwa. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

<sup>237</sup> [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . manja anu, ndipo iyimbeni iyo tsopano.

Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomane . . .

<sup>238</sup> Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Kelly. Ndine wokondwa kukuonani kuno! [Mlongo Kelly akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Kulondola. Mulungu akudalitseni.

<sup>239</sup> Nonse mukudziwa amene akufuula uyu. Ndi Mlongo Kelly. Inu mukudziwa, iye anali ku. . . A—mdierekezi anayesera kumupha iye kunja kuno, mu ngozi ya galimoto, ndipo anamutengera iye kunja uko ku chipatala, atadulidwa yense, ndipo anati iye sadzayendanso, ndi chirichonse. Koma, chisomo cha Mulungu! Iye anali amene anachiritsidwa. Zikumveka ngati a Salvation Army kuno mmawa uno. Tiyeni tilemekeze Ambuye ndi iye, aliyense! Nonsenu bwerani, mudzakumane ndi Mlongo Kelly, ndipo mudzigwirana naye chanza pamene inu mukubwera.


<sup>240</sup> Ndikudziwa kuti ndinu nonse okondwa kumuona mlongo wanu. Ndipo, apa, tsikirani mmusi ndi kudzagwirana naye chanza, pomwe pano apa pa guwa. Inu nonse mutero, aliyense. “Wokondwa kukuonani inu!” Chabwino, Ambuye alemekezeke!

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!  
 Mulungu akhale nanu mpaka  
 tidzakomanenso!

M'bale Neville.

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!  
 Mpaka tidzakomane pa mapazi a Yesu; (Mpaka  
 tidzakomane!)  
 Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!

Mulungu akudalitseni, M'bale Neville. Ameni. Mulungu akudalitseni.

<sup>241</sup> Tiyeni tiyimire ndipo tiweramitse mitu yathu miniti yokha, inu mutero, pamene m'bale akutibalalitsa. Weramitsani mitu yanu miniti yokha mu pemphero. M'bale Neville, ngati inu mungathe. 

56-0603 Bukhu La Moyo Wa Mwanawankhosa  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)